


**TRUTH
CENTERED
TRANSFORMATION**

MODULE 2



UFUMU WA MULUNGU

BUKU LOPHUNZITSIRA



Truth Centered Transformation - Module 2: Kingdom of God Copyright ©2012^{SEP} Reconciled World, Phoenix, Arizona, United States of America. www.reconciledworld.org

This work is made available under the terms of the Creative Commons Attribution-ShareAlike 3.0 license. You are permitted and encouraged to adapt the work, and to copy, distribute, and transmit it under the following conditions:

Attribution -- You must attribute the work by including the following statement: Copyright © 2012. Published by the Reconciled World (www.reconciledworld.org) under terms of the Creative Commons Attribution-ShareAlike 3.0 license. For more information, see www.creativecommons.org.

Non-Commercial -- You may not use this work for commercial purposes.



If you are interested in translating this material, please contact info@tctprogram.org.

All scripture quotations, unless otherwise indicated, are taken from the Holy Bible, New International Version®, NIV®. Copyright ©1973, 1978, 1984, 2011 by Biblica, Inc.TM Used by permission of Zondervan. All rights reserved worldwide. www.zondervan.com The “NIV” and “New International Version” are trademarks registered in the United States Patent and Trademark Office by Biblica, Inc.TM

KUTHOKOZA

Ziganizo za mu phunzilo limeneli , si zanga. Mwa nthawi zonse , ndikudalilila pa ena amene atsogola pamaso panga. Mwa ichi , zomwe ndakonzazi zachokera mu ntchito ya DISCIPLE NATIONS ALLIANCE (disciplenations.org). Mipingo yambiri imene yaphunzila izi athandiza kukonzanso mwina ndi mwina kudzera mu kupeleka zotsatira za zimene apeza kapena zimene zinawasokoneza. Kuthokoza kwanga kupite kwa iwo chifukwa cha kusatopa kwawo ndi ine pa nthawi imene ndimaphunzila kulumikiza choonadi kuti chikhale mwa njira yomwe anthu atha kuimvetsetsa mosavuta.

Zambiri za phunzilo limeneli zatengedwa mbuku la Bob Moffit mutu wake ndi “CHIKHALA YESU NDI MEYA” Ziganizo komanso zithunzithunzi mu phunzilo 2,5 ndi 6 zatengedwa mbuku limeneli. Phunziro 3 , zofunika zambiri zatengedwa buku lothandizila awerengi a baibulo “God’s unshakeable truth”(Kingdom Lifestyle Bible Studies)imene analemba Bob moffit ndi Scott Allen.

Ngakhale zonsezi zachokera kwa anthu ena , koma zolakwikazo ndi zanga , chonde mundiziwitse ngati pali pena pomwe palakwika. Ndidziwitseninsu ngati pali ziganizo zina zabwino zomwe tingatukulile phunzitori.

ZAMKATIMU

Phunziro 1: Ufumu wa Mulungu	8
Kodi Ufumu wa Mulungu ndi Chiyani.....	8
Kumvera mu Zinthu Zonse	9
Kumanga Ufumu wa Mulungu	10
Phunziro 2: Madera a Ufumu	11
Ufumu Padziko Lapansi	11
Mulungu ngati Olamulira Madera	12
Yesu ngati Mtsogoleri Wadera	12
Kusintha kwa Dera Mzigawo Zinayi.....	13
Phunziro 3: Zoyenera Ufumu	15
Zoyenera Kuchita Pachiyambi	15
Kugwiritsa Ntchito Baibulo Mzigawo Zonse Za Moyo Wathu	17
Kupeza Zomwe Mulungu Amafuna	19
Phunziro 4: Zoyenera Ufumu ndi Ntchito	20
Chiyambi	20
Zomwe Baibulo Limakamba Zokhudzana ndi Ntchito	21
Mitundu ya Ntchito	21
Mulungu Amasla Mmene Timagwilira Ntchito	23
Phunziro 5: Kumanga Ufumu wa Mulungu	26
Zimayamba ndi Ife.....	26
Dera Losinthika.....	26
Kodi Tingasinthe Dera Lathu?	27
Mbale Lawrence.....	29
Kuchoka kwa Anthu Kupita ku Mbanja ndi ku Madera	29
Mabanja	29
Madera.....	30
Zitsanzo Zina za Anthu Omwe Anamanga Ufumu wa Mulungu	32
Mungakhale Bwanji Omanga Ufumu	34
Phunziro 6: Udindo wa Mpingo Pomanga Ufumu wa Mulungu.....	36
Chiyambi	36
Kuthandiza Anthu.....	37
Kodi Mchifukwa Chiyani Aliyense Akuyenera Kutumikira?	37
Kusintha Mabanja	39
Kusintha Madera	39
Phunziro 7: Pulogalamu ya Truth Centered Transformation.....	42
Masomphenya a Pulojekiti.....	42
Kutukula Mipingo	42
Kusintha Madera	43
Zigawo Zosintha	44

Njira.....	44
Maphunziro a Mtsogolomu.....	45
Phunziro 8: Zotsatira	47
Kodi Kukonzekera Mkofunika Motani	47
Mikumano	48
Ntchito za Chikondi	48
MACHITACHITA A CHIKONDI- MNDANDANDA WA ZOCHITIKA.....	49

Musanayambe

Kukonzekera kuphunzitsa phunziro

- Werengani **Buku la Aphunzitsi** mofatsa, ndipo mubweleze ngati mkotheke. Lembani mzere kungsi kwa mfundo zofunikira kapena zilembeni mbali mwa buku kuti muzikumbukile mosavuta.
- Onetsetsani zolinga za phunziro lililonse kuti mudziwe zomwe ophunzira akuyenela kuphunzira paphunziro limenelo.
- Welengani malemba onse ogwilizana ndi phunziro pokonzekera.
- Funani zipangizo zomwe zingafunike pa phunziro lililonse ndipo onetsetsani kuti mwakonzaz mapepala othandizila ophunzira komanso kupanga zithunzi zophunzitsila.
- Onetsetsani kuti mukudziwa zonse zochitika mu phunziro (sewero, zithunzi zothandizila phunziro). Mutha kuyesa zochitikazi ndi anzanu kapena akubanja lanu.
- Mukhale ndi nthawi yopemphera pokonzekera phunziro, kuti ophunzira amvetse chifuniro cha Mulungu komanso kuti Mulungu akuthandizeni pophunzitsa. Kumbukilani kuti ndi mphamvu za Mulungu zokhazomwe zingasinthe anthu.

Mfundo zothandiza kuti kuphunzitsa kukhale kopambana

- Fikani mwachangu ndipo konzani zipangizo zophunzitsira komanso malo omwe mugwilitse ntchito.
- Musaphunzitse mothamanga. Ikani nthawi yokwanila ya zokambilana, ntchito ndi nthawi yopumila. Cholinga ndichoti anthu akhale ndi nthawi yokwanila kumvetsa ndi kutenga mbali pa phunziro. Yendani pa mlingo wabwino kuchoka phunziro kupita lina kuti aliyense amvetse. Maphunziro ena akhoza kutenga theka kapena tsiku lina loonjezela.
- Unikilani pafupi pafupi. Pachiyambi paphunziro latsopano bwelezani zomwe zaphunzitsidwa kale. Kubweleza kumathandiza ophunzira kuti akumbukile zomwe aphunzitsidwa.
- Tsatilani Buku la Aphunzitsi komanso konzani zokuthandizilani kuphunzitsa.
- Onetsetsani kuti magawo onse anayi ofunika pa phunziro akupezeka
 - Lankhulani mau oyambila phunziro – izi zimalumikiza mutu wa phunziro ndi zomwe ophunzira akudziwa kale
 - Perekani mfundo zatsopano –pali njira zambiri zopelekera mfundo zatsopano.
 - Uzani ophunzira mfundo zina pophatikiza zomwe aphunzira – izi zimawathandiza kuti amvetse pogawana mfundo ndi anzawo, kubwela ndi mfundo zina kapena kugwilitisa ntchito mfundo zatsopano munjira ina.
 - Lumikizani mfundo ndi moyo wao – iyi ndi gawo lomwe limathandiza ophunzira kuti alingalire njira zogwilitira ntchito mfundo zomwe aphunzirapamoyo wao. Ngati zophunzitsidwa sizikugwilitidwa ntchito sizibweletsa kusintha ndipo sizithandiza kwenikweni.

- Unikilani zofunika kuphunzitsira akulu ndi luso lina lomwe linaphunzitsidwa pa maphunziro a aphunzitsi.
 - Perekani njira/mbali zoyenela kutsatidwa
 - Funsani mafunso omwe angapangitse ophunzira kupereka maganizo awo
 - Kumbukilani kuthokoza ophunzira chifukwa chotenga nao mbali
 - Musawauze ophunzira zomwe angaphunzire pochita kafukufuku
 - Gwilitsani ntchito zomwe anthu akudziwa kale ndipo dziwani kale lao
 - Khalani odekha, dikilani kuti anthu apereke mayankho
- Kulimbikitsa aliyense kutenga nao mbali, kugawana ndi kupeleka ndemanga zothandizila zokambilana. Pezani njira zothandiza kuti anthu amanyazi athe kutenga nao mbali
- Pempherani kwa Mulungu tsiku lonse kuti apeleke nzeru zatsopano kwa inukomanso ophunzira.

Kagwilitsidwe Ntchito ka Buku Ili

- **Zolinga ndi zipangizo:**Phunziro lililonse likuyamba ndi gawo lino
 - **Zolinga**—ophunzira akwanilitse izi kumapeto kwa phunziro. Ndibwino kudzifunsa ngati zolingazi zakwanilitsidwapamapeto pa phunziro. Bwelezani mfundo zofunikila (zikuluzikulu) kuti ophunzira adzikumbukila.
 - **Zipangizo**—Zipangizo zofunikila pa phunziro lililonse zilembedwe, kuphatikizapo zithunzi ndi mapepala a ophunzira. Muthakupeleka mapepala othandiza ophunzira kwa aliyense kapena owelengeka monga mwakonzera pa phunziro lililonse. Ndibwino kugwilitsa ntchito chithunzi kapena bolodi pophunzitsa gulu lalikulu.
- **Malangizo a aphunzitsi:** Pali malangizo apadera a aphunzitsi okuthandizani mutsogolere bwino phunziro. Malangizowa sioyenela kugawana ndi ophunzira. Muwelenge malangizowa pokonzekera phunziro. Mafunso ena ali ndi mayankho okuthandizilani ngati mphunzitsi. Mayankho amenewa ndi poyambila, mutha kupezanso mayankho ena oonjezela abwino.
- **Kasungidwe ka nthawi ndi kayendedwe ka phunziro:** Phunziro lililonse silinapatsidwe nthawi yokhazikika.
 - Tengani nthawi yokwanila kuti muthandize anthu kumvetsa phunziro. Mkofunika kukhala okhudzika ndi zomwe anthu aphunzirakusiyana ndi kumalizitsa phunziro munthawi yoikika.
 - Kumbukilani kupeleka mpata kwaanthu kuti ayambe ndi matamando, kugawana maumboni, ndikukambilana mavuto omwe akukumana nao komanso kupemphera limodzi.

Phunziro 1: Ufumu wa Mulungu

Zolinga

- Kudziwa kuti Ufumu wa Mulungu umadza (umapezeka) tikamvela kwathunthu malamulo a Mulungu
- Kudziwa kuti Ufumu umakula anthu ambiri akamvera Mulungu ndipo tikamumvera lye kwathunthu

Zipangizo

- Palibe

Ufumu wa Mulungu ndi Chiyani?

Mmene Yesu anali padziko lapansi anafotokoza za pulani lake. Pulaniyi ikufotokozedwa mu Chipangano Chatsopano mokwana nthawi makumi asanu ndi anayi kudza kasanu ndi kanayi (98). Yesu akulankhula kuti lye anadza chifkuwa cha pulaniyi, ndipo anatuma ophunzira ake kukaphunzitsa za pulaniyi. Paulo analankhula za pulaniyi ndipo tikulimbikitsidwa kuipemphelera.

- Kodi mukuidziwa?

KAMBILANANI PAGULU

Welengani mavesi otsatilawa ndipo muyankhe mafunso:

- Mateyu 10:5-8 — Kodi Yesu adawatuma ophunzira ake kuti akaphunzitse uthenga otani?
- Luka 4:43 — Mchifukwa chiyani Yesu anatumidwa?
- Macitidwe 1:3 — Kodi Yesu anaphunzitsa zotani masiku ake makumi anayi akumapeto padziko lapansi?
- Macitidwe 28:30-31 — Kodi Paulo anaphunzitsa zotani?

Pulani ya Mulungu ndikumanga Ufumu wake. Monga tikuonela mmavesiwa, iyi ndiyo mfundo yaikulu yomwe Yesu ndi Paulo anaphunzitsa. Ikuyenela kukhala yofunikila kwaifenso. Komabe, ambiri sitimvetsa tanthauzo la mau oti “Ufumu wa Mulungu.”

Taganizani za winawake ndipo mulingalire za mmene mungafotokozere za Ufumu wa Kumwamba kwa mkhristu watsopano.

Fotokozani mayankho kwa gulu lonse.

Ufumu wa Kumwamba siovuta kuulongolosola. Ufumu wa Kumwamba uli paliponse pomwe Yesu ndi Mfumu ndipo malamulo ake akutsatidwa. Ndiye tikaona anthu akumvera Mulungu ndikutsata chifuniro

chake, pali gawo la Ufumu wa Mulungu. Tchutchutthu wake ndiwakuti Ufumu wa Mulungu sungadze kwathunthu kufikira Yesu atabweranso kachiwiri ndipo zinthu zonse zitapangidwa kukhala zatsopano komanso tchimo kulibe.

Kuti timvetsetse izi tiyeni tilingalire za dziko la Thailand. Thailand ndi dziko lomwe limalamulidwa ndi mfumu; ali ndi mfumu ndipo mfumuyo ikayankhula anthu amamvetsera. Mfumuyi inati imakonda zamaonekedwe achikasu, ndipo pakadali pano anthu amdzikoli amavala Malaya achikasu Lolemba lililonse. Mfumuyi inati mkazi wake amakonda za mtundu okhathamira (purple), ndipo pakadali pano anthu amdzikoli amavala Malaya amtunduwu Lachisanu lilonse. Iyeyu amakondedwa kwambiri ndi anthu a mdziko lake kotero kungonena zamtundu umene amakonda, zimakhudza mmene anthu amavalira.

Zaka zingapo zapitazo, asilikali analanda dziko la Thailand. Kunali kumenyana mmizinda ndi malo ena. Omwe anali kumbuyo kwa Boma anamenyana ndi omwe anali kumbuyo kwa asilikali. Kenako mfumu idayankhula. Iyo inalamula kuti asiye kumenyana kuti pachitike masankho. Kumenyanako kunatha nthawi yomweyo. Palibe yemwe anaifunsa Mfumu; iwo anangopanga zomwe Mfumu inalankhula. Ngakhale ena anali okwiya, sizinawakhudze. Mfumu inalankhula ndipo kusangalatsa Mfumu kunali koposa mmene amamvera.

Tilinayonso Mfumu – Yesu ndiye Mfumu yathu. Kodi sikoyenela kuti timusangalatse (Yesu) ndikuchita monga amachitira anthu a mdziko la Thailand posangalatsa Mfumu yao? Ngati anthu a ku Thailand amakonda Mfumu yao kwambiri kufika poti mtundu omwe amakonda umakhudza mmene anthu angavaliye, kodi sikoyenera kuti miyoyo yathu ikhudzidwe ndichikondi cha Mfumu yathu Yesu?

ZOKAMBILANA PA GULU LALIKULU

- Kodi timafuna kukondweretsa Mfumu yathu muzochita zathu zonse? Chifukwa chani timatero kapena timalephera?
- Kodi ndi magawo ati mmiyoyo yathu omwe titha kuphunzira kumvera Mulungumopambana?

Kumvera mu Zinthu Zonse

Mulungu akufuna kuti timukondweretse ndikumulemekeza lye nthawi zones. Werengani Akolose 3:17 ndi 1 Akorinto 10:31. Mavesi amenewa akutiya kuti muchilichonse chomwe tingachite, kuti tibweletse ulemelero kwa Mulungu. Mavesi onse akubweleza ganizo loti muntchito zathu zonse: ku Akolose, “Ndipo chilichonse mukachichita **m’mau** kapena **muntchito**, chitani zonse m’dzina la Ambuye Yesu, ndi kuyamika Mulungu Atate mwa lye. Ku Akorinto, “Chifukwa chake mungakhale mudya, mungakhale mumwa, mungakhale muchita kanthu kena, chitani zonseku ulemelero wa Mulungu.” Ngati mau abwezedwa mbaibulo, zimasonyeza kuti ndiofunika. Paulo akufuna kuti timvetse kuti MUCHILICHONSE ulemelero ukuyenela kukhala kwa Mulungu.

ZOKAMBILANA GULU LALIKULU

- Kodi ndi zinthu zANJI zomwe timapanga patsiku? (Lembani ndandanda wa zochitikazi pabolodi).
- Kodi tingadzetse bwanji ulemelero kwa Mulungu pomwe tikuchita chilichonse mwa ntchito tatchulazi? (yankhani potsatira ndandanda omwe mwalembe).

Tikuyenela kudzikhuthula pakumvera Mfumu yathu Yesu ndikumukondweretsa Iye. Mulungu watipangira zambiri, kutumiza mwana wake kudzatifera. Tikamasinkhasinkha za mphatso yamtengo wapatali imeneyi tikuyenela kukhala ndi chikhumbokhumbo chomvera malamulo ake.

Mangani Ufumu wa Mulungu

Werengani Mateyu 6: 9-10

- Kodi Yesu akuti tidzipemphelera chiyani?
- Kodi tikuona kuti Ufumu wake ungadze motani?

Mulungu akufuna kumanga Ufumu wake padziko lapansi. (Ufumu wanu udze.) Ufumu wake wamangidwa padziko lapansi ndi anthu omwe akuchita chifuniro chake. (Kufuna kwanu kuchitidwe.)

Pali njira ziwiri zomwe tingamangire Ufumuwa Mulungu. Njira yoyamba ndikuchulukitsa chiwerengero cha anthu opulumutsidwa muufumu wake. Njira yachiwiri ndikuthandiza anthu kuchita chifuniro chamulungu kawirikawiri. Monga tinaphunzilira, Yesu anadza kudzayanjanitsa zinthu zonse (Akolose 1:18 -20).

Ngati tikufuna kuti chifuniro chamulungu chichitike kopambana, tikuyenela kuthandiza anthu kuti apulumutsidwe komanso amvere Mulungu, ndipo tikuyenela kuthandiza anthu kukhala monga Mulungu akufunira muzigawo zonse zamiyoyo yathu.

Phunziro 2: Madera a Ufumu

Zolinga

- Kumvetsetsa ngati tikukhala moyo omvera, tikuyenera kuthandiza dera lathu kukhala lofanana ndi Ufumu wa Mulungu.

Zipangizo

- (HANDOUT 2.1)Nkhani za mdera
- Mapepala aakulu
- Zeken

Ufumu Padziko Lapansi

Taganizani za momwe zingakhalire Ufumu wa Mulungu utakhala padziko lapansi? Mu Chipangano Chatsopano timaona zitsanzo zambiri za chiyanjano cha Akhristu oyambakupanga Ufumu wa Mulungu.

Werengani Machitidwe 2:42-47

- Kodi okhulupilira atsopano anachita chiyani?
- Kodi izi ndizauzimu kapena kuthupi? (Zonse)
- Kodi zotsatira zake zinali zotani?
 - *Panalibe osowa, anthu ena anawayang'ana mwachimwemwe, ndipo anthu ambiri anakhulupilira.*
- Kodi ndizotsatira zotani zomwe tingazione mmadera athu nthawi timakhala pamkumano ngati okhulupilira akale amachitira?

Mulungu ngati Olamulira wa Madera athu

Mulungu akufuna madera athu adzikhala monga mmene lye amafunira. lye sakungofuna kuti chifuniro chake chichitike mmiyoyo yathu patokha, koma dera lathu lonse.

MMAGULU AANG'ONO

Malangizo: Werengani nkhan yotsatilayi ndipo muyankhe mafunso (HANDOUT 2.1)

Bambo ena mdziko la india anapita kumudzi wina komwe ankagwila ntchito. lye anafunsa azimayi a mmudzimo kuti kodi mudzi wao ukadaoneka motani ngati Yesu atakhala mtsogoleri mmudzimo. Umrai, mmodzi mwa azimayi okonda kulankhula mwa tchutchutchu (mosapsatira mau), anafotokoza mmudzi omwe uli wagwilizano ndi kulolerana.

Mayiyu anadziwa zoti Yesu salemkezedwa kamba ka kugawanikana kwa anthu a mmudziwu. Chifukwa cha kuyankha kwake, gulu la azimayi mmudziwu linayambitsa komiti lazaumoyo ndi gulu lodzithandiza lokha. Gulu la azimayi khumi ndi anayi (14) lodzithandiza palokha lija linayamba kukumana pafupipafupi komanso linali lachidwi. Mamembala aguluri anatolera ndalama ndikuzisunga kuthumba lagulu ndipo anayamba kuthana ndi mavuto ochitika mdera lao limodzi. Umrai, anakhala Pulezidenti (Mtsogoleri) wakomitiiti ndipo anagwilitsa ntchito mphatso yake yautsogoleri posonkhanitsa anthu kugwila nthcito zomwe Yesu akanapanga akanakhala mtsogoleri.

Azimayi ena ophunzira Baibulo ku Uganda anaganiza kutumikira mudzi wao monga akanachitira Yesu. Iwo anakonza dongosolo la pulojekiti loyamba: kuchotsa zinyalala panja pamalo ena omwera mowa. Azimayi ena awiri olimba mtima analowa mmalo omwera mowawo. (Mwachizolowezi, azimayi omwe amapita kumalo omwera mowa ndi oyendayenda {mahule}). Iwo anapempha chilolezo kuti achotse zinyalala. Eni ake omwe amadabwa ndi zochitikazi anawaseka komabe anawalora kutero. Azimayiwo anasonkhanitsa anthu mdera lozungulira, ndipo anthu ambiri anadzipeleka. Gululo linakumba mayenje awiri: limodzi lotayila zinyalala zoyanjana ndi zachilengedwe ndi lina lotayila zinyalala zosayanjana ndi zachilengedwe. Oyangani pa malo omwera mowawa ataona anthu ena akukonza pamalopo anawathandiza. Mosangalatsa anthu amderali, eni ake amalowa anapitiliza kukonza malowa paokha.

Chifukwa cha kulimbikitsidwa, amayiwa anaganiza zomanga malo ophikira oyendera mafuta asanu ndi anayi (9) kwa mawanja amderalo ndi kupeleka zosungira madzi kwa anthu osowa. Kenako gulu lophunzira Baibulo linakula mkupanga pulojekiti yaikululu: msika. Azimayi ammudzi ankayenda maola ambiri, atanyamula masamba ndi katundu wina kukagulitsa kumisika yakutali. Msika wapafupi unawathandiza kuti apeze phindu komanso kukhala pafupi ndi mawanja awo, dera lao, ndi minda yao. Anthu anapatsidwa malo koma anali otsetseleka kotero kunali kovuta kuti ayambe kumanga msika. Azimayi a gulu lophunzitsa Baibulo anapemphera ndipo okonza mseu omwe amakonza mseu wapafupi anabwera modzipereka ndikukonza malowo popanda cholowa (ndalama). Ndi chithandizo cha Mulungu kagulu kakang'onoka azimayi achikhristu akumudzi anasonkhanitsa zinthu, ndalama, anathana ndi mavutondikumanga msika mdera lao. Moyo wao wauzimu unakula kamba kothandiza anthu ena mmalo mwa Yesu.

Kambilanani:

- Kodi zomwe zinachitika mu nkhani zonse ndizotani?
- Chifukwa cha anthu munkhanizi, kodi maderawa anayandikira pafupi ndi momwe zikanakhallira ngati aliyense akanakhalamonga Yesu akufunira? Mchifukwa chiyani?
- Kodi zina mwazomwe mwapanga pagulu ndichani?
- Kodi mungapange motani zinthu zienezizi mdera lanu?

Yesu ngati Mtsogoleri wa mdera

GULU LALIKULU

Tangoganizani Yesu ali mtsogoleri wadera lanu. Mukuganiza kuti zinthu zoyambilira kuti iye asinthe zingakhale chani?

Malangizo:Ngati gulu likukhaizikika kwambiri pakusinthatsogoleri andale, akumbutseni kuti mmene Yesu anali padziko lapansi sanasinthe atsogoleri andale.Ophunzira ake amayembekezera kuti athana ndi maukulu azandale; koma Iye sanatero. Anagwira ntchito ndi anthu kuti adzetse kusintha. Mupulogalamu iyitikhazikikapounikila pazakukhala monga Mulungu akufunila komanso kuthandiza ena kuchita chimodzimodzi.

Ngati gulu likukanika kuganiza mutha kufunsa mafunso awa kuti zokambilana ziyambike:

- Kodi Yesu amatani nao azimayi amasiye ndi ana amasiye?
- Kodi Iye angatani kuti alimbitse mabanja?
- Kodi Iye angalimbikitse motani kumwa madzi aukhondo, kukhala ndi nyumba yabwino ndi chakudya, zaumoyo, zokhudzana ndi kusamala zinyalala, ndi miseu yabwino?
- Kodi chingachitike ndichani ndi maphunziro a ana komanso akuluakulu?
- Kodi Iye angatani ndi uchidakwa, kugwilitsa ntchito mankhwalawosokoneza bongo, njuga, ndi makhalidwe ena osayenera?
- Kodi Iye angatani ndi nkhanza za m'banja komanso nkhanza kwa ana?
- Kodi Iye angatani kuti alimbikitse ubwenzi pakati pa anthu?

Kusintha kwa Dera Muzigawo Zinayi

- Mukukumbukila njira zinayi za momwe tingakulire monga Yesu anakulira? (Luka 2:52)
 - Mnzeru,Thupi,Kuyanjana ndi ena (chisomo cha pa anthu) ndi Uzimu

Ufumu wa Mulungu umadzetsa kusintha mmagawo anayi. Ngati tikufuna dera lathu kukhala ngati Ufumu wa Mulungu, tikuyenera kuganiza za kusintha mmagawo anayi mdera lathu.

MMAGULU AANG'ONO

Malangizo: Gawanikalasi mmagulu ndipo muwauze kuti akambilane za momwe dera lapamwamba lingakhalire kapena kuonekera. Makamaka muwafunse kuti alingalire zauzimu, kuthupi zachiyanjano ndi anthu ena komanso zakaganizidwe. Muwafunse kuti akhale ndi chithunzithunzi cha zomwe akuganiza zokhudzana ndi momwe Mulungu angafunire kuti dera lao likhale lotani.

Fotokozani:

Mulungu amafuna kuti madera omwe tikukhala asinthe ndikukhala ngati Ufumu wake. Iye anatilimbikitsa kuti tipemphere za kudza kwa Ufumu wake padziko lapansi monga kumwamba ndipo anatiuza kuti tiyambe tathanga (tafuna) Ufumu wake.

Talingalirani kuti zingakhale motani kuti tikhale mmadera omwe aliyense akukhala momvera Mulungu kwathunthu? Kungakhale mabanja achimwemwe, anthu oyandikana nao ochezeka, kuthandizana wina ndi mnzake kukhala mumtendere; sikungakhale kukangana kapena kumenyana komanso chinyengo. Mungakonde kukhala dera ngati limenero?

Njira za Mulungu zodzetsa Ufumu wake ndikudzera mwaife. Tiphunzira mu phunziro 4, koma pakadali pano tiyeni tilingalire za: *(Werengani zotsatilazi pangonopangono kupereka mpata kwa anthu kuti asinkhesinkhe za mayankho.)*

- Kodi chingachitike ndichani kuti kuyambila mmawa mammawa, 6 koloko, aliyense ayambe kuonetsa khalidwe monga Mulungu amafunira?
- Kodi chingachitike ndichani kwaife, aliyense payekha, ngati tingamvere zofuna za Mulungu pamaubale athu, kusamalira matupi athu, ndi kuyenda kwathu ndi Mulungu?
- Kodi chingachitike ndichani ku mawanja anthu ngati tonse m'banjamo tikumvera zofuna za Mulungu kwathunthu ndimaubale pakati pa wina ndi mnzake?
- Kodi chikanachitika ndichani mumpingo mwathu ndi mmipingo ina yamdera lathu ngati pakankhala chikondano pakati pa wina ndi mnzake kwa azitsogoleri ndi mamembala, kutumikirana, kusamalira ovutika ndi osauka ndikukhala muumodzi?

Mulungu watipatsa masomphenya osangalatsa: masomphenya a kudza kwa Ufumu wake padziko lapansi. Iye akufuna kuti titenge nao gawo pomanga Ufumu wake padziko lapansi. Talingalirani za momwe dziko lingakhalire ngati aliyense atamvera Mulungu. Ikhala kumwamba! Ngakhale tikudziwa kuti sitingamalizitse mpaka kubweranso kwa Yesu, titha kuyamba kugwira ntchito pofuna kukwanilitsa masomphenya a Mulungu.

Tsiku lililonse tikuyenera kudzuka ndikulingalira kuti tingamange motani Ufumu wa Mulungu lero? Kodi ndingatani kuti ndionjezele Ufumu wa Mulungu? Kodi ndingakhale bwanji kuti ndikhale mwa malamulo a Mulungu? Ndingathandize bwanji apabanja langa kuchita chimodzimodzi?

Phunziro 3: Zoyenera Muufumu

Zolinga

- Kudziwa kuti mavuto a mdera lathu atha kuthetsedwa kudzera pakumvera Mulungu kwathunthu.
- Kuzindikira kuti Ufumu wa Mulungu umadza tikamagwilitsa ntchito Baibulo muzonse pamoyo wathu.
- Kuzindikira kuti zoyenera kuchita motsatana ndi Baibulo ndizosiyana ndi zoyenera kuchita za mmadera athu.
- Kudziwa kuti titha kupeza zoyenera kuchita mbaibulo tikawerenga Baibulo.

Zipangizo

- Handout 3.1 ya Zoyenera Muufumu ya Mafunso
- Maposita a zoyenera kuchita pachiyambi

Zoyenera kuchita pachiyambi

Tiyeni tiyambe ndikuona zoyenera kuchita zitatu zoyambilira.

Dziko lapasuka kwambiri. Nzeru za anthu a dziko lapansi ndi zipangizo zadziko lapansi sizingathe kukonza dzikoli.

- Kodi zina mwa zitsanzo za zotsatira za tchimo ndichani padziko?

Ena mwa mayankho

- *Kumwa mowa mwauchidakwa/juga/uhule*
- *Kupasuka kwa mawanja*
- *Kumenyana kwa anthu*

Werengani nkhani yotsatirayi:

Dziko la Haiti ndi limodzi mwa zitsanzo za chipasuko chomwe nzeru za anthu komanso zipangizo zalephera kukonza. Haiti ndi dziko losaukitsitsa kumwera ndi pakati padziko la America. Ili ndi anthu okwana 8 miliyoni. Kuyambira chaka cha 1980, mapulogalamu zikwizikwi a mabungweapadziko lonse, mabungwe aboma komanso a mabungwe oyima paokha achitika. Madola mabilyoni agwira ntchito kulimbikitsa zachuma, zokhudzana ndi anthu komanso zauzimu mdziko la Haiti. Ngakhale zili chomwechi palibe chasintha. Mchaka cha 2004 mabungwe apadziko lonse ndi boma anapeleka madola bilyoni imodzi kuthandiza kukonza zinthu mdziko la Haiti.

Ngakhale pali ndalama izi zankhaninkhani, dziko la Haiti silinasinthe. Anthu akuvutikabe; alibe chiyembekezo. Anthu 80 peresenti ali paumphawi waadzaoneni. Kulibe mafakitale ndi malonda mdzikolo; zonse zinatsekedwa. Vuto lakusowa ntchito liri pafupifupi 70 peresenti. Ana opitilira 10 peresenti sakhala ndi moyo kupitilira zaka zinayi. Zisakasa za nyumba ndizochuluka, anthu alibe malo okhala okhazikika ndipo miseu yambiri ndiyod zadza ndi zinyalala. Ziwawa zimachitika popanda ch

itetezo. Miseu inaonongeka ndipo palibe madzi akumwa okwanira. Madera akumidzi nao sali bwino. Patadutsa zaka zingapo mitengo inadulidwa mosasamala ndipo nthaka inakokoloka, mmidzi ilibe zodzitetezera kumphepo yamkuntho ndipo palibe malo anthaka yachonde yoyenera ulimi.

Ngakhale ndalama zaonongedwa ndi nzeru za akatswiri, palibe kusintha. Zipangizo zachumasizinathandize kukonza malo ngakhale nzeru za akatswiri apadziko lapansi.

- Kodi zinthu zili bwanji ku Haiti?
- Kodi ku Haiti kumaonongedwa ndalama zingati?
- Kodi izi zimadzetsa kusintha kotani?
- Mchifukwa chiyani mukuganiza kuti izi zili choncho?

Dziko lapasuka (laonongeka) ndipo magazine athu abwino siokwanira kukonza dzikoli. Ku Haiti, Ngakhale madola mabiliyoni ndi zikwizikwi za akatswiri zalowelerapo, zinthu sizinasinthe. Izi zikuchitika padziko lonse osati ku Haiti kokha ayi. Pakutha kuononga (kugwiritsa ntchito) madolamabiliyoni makumi asanu (50) ku Africa ndikutumiza akatswiri zikwizikwi, dzikoli ndilosauka kwambiri kusiyana ndi momwe inalili zaka 20 zapitazo. Nzeru zaanthu ndi zipangizo ndizosakwanira kuchiza nthenda (kuthetsa mavuto) ya adzikoli. Tikufunika chinachake.

Kuchiza dziko kumachitika kudzera mwa anthu akamatsatira Mulungu ndikukhala mmalamulo ake.

Werengani 2 Mbiri 7:14

- Kodi Baibulo ikuyankhula kuti tikuyenera kutani?
- Kodi akufunira izi ndani –akhristu kapena akunja?
- Kodi chingachitike ndichani tikatsatira izi?
- Mukukhulupilira kuti vesili likukamba zoona?
- Kodi tikuyenera kutani kuti tione madera athu atachiritsidwa?

Mulungu akufuna kuti madera athu achiritsidwe. Yesu anabwera kudzayanjanitsa zinthu zonse. Komabe, Iye amagwira ntchito kudzera mwaife. Popanda kupemphera, kusala kudya, ndikuyenda moyo omvera Mulungu machiritso sangabwele! Machiritso a Mulungu ku madera athu amadza tikapanga zinthu izi. Kodi mukufuna machiritso a dera lanu? Mwakonzeka kupanga zinthu izi?

Baibulo limatiuza mmene tingakhalirekuti tichiritse maiko athu ndikumanga Ufumu wa Mulungu.

Nthawi zina tikagula katundu wamtengo wapatali amatipatsa kabukukofotokoza mmene tingagwilitsire ntchito katunduyo. Kabukuka kamalembedwa ndi kampani yomwe yakonza katunduyo. Iwo amadziwa

mmene katunduyo akuyenera kugwiritsidwira ntchito kuti agwire bwino ntchito komanso kuti akhale nthawi yaitali. Ngati tikufuna zotsatira zabwino pakatunduyo tikuyenera kuwerenga kabuku kameneka.

Mulungunso ndi chimodzimodzi. Anapanga ndikulenga dzikoli. Anapanganso ife. Amadziwa kupanga dziko ndi miyoyo yathu kuti ikhale bwino ndipo lye walemba buku lamalangizo ammene tingakhaliwe. Imatchedwa Baibulo. Mbaibulo amatiuza mmene tikuyenera kukhalira mbali zonse za moyo wathu. Baibulo ili ndi mmalamulo onse ndi nzeru zomwe tikuzifuna kuti tichiritse dziko ndi madera athu opasuka. Tikuyenera kuwerenga, kumvestetsa ndi kugwiritsa ntchito zolembedwa mbaibulo muzonse ngati tikufuna kusintha miyoyo yathu ndi madera athu.

Malangizo: Bwerezani maganizo awa pogwiritsa ntchito makadi. Onetsetsani kuti kalasi lamvetsa kadi iliyonse.

- Kodi taphunzira zotani zokhudzana ndi mmene tingachizire dziko?
- Kodi tingayende bwanji momvera Mulungu?
- Tikuyenera kuwerenga Baibulo ndikuligwiritsa ntchito muzonse.
- Kodi Mulungu watilonjeza zotani ngati tingakhale omvera?

Kugwiritsa Ntchito Baibulo Mbali Zonse Zamoyo Wathu

Mukawerenga nkhani zokhudza Yesu anali padziko lapansi mupeza kuti ophunzira ake anali ndi malingaliro ena pa momwe Yesu ankalamulira kusiyanana ndi momwe lye anachitira.

Werengani Marko 10:35-37,41-45

- Kodi Yakobo ndi Yohane amakambirana zotani?
- Kodi Yesu analankhula zotani zokhudzana ndi momwe atsogoleri akuyenera kukhalira?

Yakobo ndi Yohane amaganiza monga mwa chikhalidwe chao. Iwo amafuna kulamulira anthu ena ndipo amalingalira za tsiku lomwe adzakhale atsogoleri akuluakulu. Koma Yesu anawakonza ndikuwauza mmene mtsogoleri wamkulu akuyenera kukhalira: mtsogoleri wamkulu ndi kapolo.

- Kodi mukuganiza kutikapolo amaoneka motani nthawi imeneyo?
- Kodi mukuganiza kuti ophunzira ake anamva bwanji atamva izi?

Izi zimachitika. Mmene dziko kapena chikhalidwe zimayendera ndizosiyana ndi Mulungu. Tikuyenera kudziwa njira za Mulungu ngati tikufuna kumanga Ufumu wa Mulungu padziko lapansi. Mulungu watipatsa baibulo, lomwe limatiuza mmene tingakhaliwe kuti tikondweretse Mulungu.

MMAGULU ANG'ONOANG'ONO

Lembani mbokosi lotsatirali (Handout 3.1). Pachilichonse ganizani za momwe chikhalidwe chanu chingakambe. Kenako yang'anani Mavesi ndikuona zomwe Baibulo likufotokoza kuti tichite.

Zoyenera kuchita	Lemba	Chikhalidwe chathu	Ufumu wa Mulungu
Kodi tikuyenera kuchita motani ngati mwamuna wapabanja	Akolose 3:17 1 Petulo 3:7 Aefeso 5:25, 28, 33		
Kodi tikuyenera kutani ngati mkazi wapabanja	Genesis 2:18 Aefeso 5:22-24, 33		
Kodi tikuyenera kuchita motani ndi ana	Masalmo 127:3 Aefeso 6:4		
Kodi tikuyenera kuchita motani ndi anthu	Mateyu 22:36-40 Luka 10:25-37		
Kodi tikuyenera kuchita motani ndi adani athu	Luka 6:27-31		
Kodi tikuyenera kuonetsa makhalidwe otani muntchito	Akolose 3:22-4:1 Aefeso 6:7-8		
Makhalidwe athu ku chilengedwe	Masalmo 24:1 Genesis 1:28-30 Genesis 2:15		
Chinthu chofunikira kwambiri	Mateyu 6:25-34 Mateyu 22:36-40		
Mmene timaonera imfa ndi kumwalira	Yohane 11:25-26 Ahebri 2:14-15 Chibvumbulutso 1:17-18		
Mmene timaonera kudwala	Luka 6:22-23 2 Akorinto 1:8-11		

Kupeza Zomwe Mulungu Amafuna

Sabata ino pamene mukuwerenga Baibulo mukuyenera kuyamba kuyang'ana zomwe Mulungu amafuna zomwe mungazigwiritse ntchito pamoyo wanu. Pamene mukuwerenga chaputala kapena ndime dzifunseni mafunso anayi awa:

- Kodi ndime iyi ikundiphunzitsa zotani zokhudzana ndi Mulungu?
- Kodi ndime iyi ikundiphunzitsa zotani zokhudzana ndi momwe ndingakhalire?
- Kodi ndimeyi ikundiphunzitsa zotani za mmene ndingachitire ndi anthu ena?
- Kodi ndimeyi ikundiphunzitsa kuti ndikuyenera kuchita motani ndichilengedwe kapena mmene ndingagwilire ntchito ndikugwiritsa ntchito ndalama ndi zina.

Phunziro 4: Zoyenera Ufumu ndi Ntchito

Zolinga

- Ntchito ndiyofunika pamoyo wathu ndipo ndiyomwe ingabweletse ulemelero kwa Mulungu. Baibulo limationetsa za momwe tingakhalire omvera pantchito yathu munjira yomwe ingadzetse ulemelero kwa Mulungu.

Zipangizo

- Handout 4.1 Zothandizira pa gulu laling'ono
- Zothandizira pantchito za John Wesley's

Chiyambi

ZOKAMBILANA GULU LALIKULU

- Kodi ntchito imaonedwa ngati yabwino kapena yoipa?
- Kodi ndimiyambi yotani muchiyankhulo chanu yokhudzana ndi ntchito?

Genesis 1:28

- Kodi malangizo oyamba omwe Mulungu anamupatsa Adamu anali otani?
- Kodi izi zimachitika asanachimwe kapena atachimwa pakudya chipatso?

Genesis 2:2

- Kodi Mulungu amapuma kuchiyani?

Marko 6:1-3

- Kodi ntchito ya Yesu inali yotani asanayambe kuphunzitsa?

Monga tikuonera Mavesi awa Mulungu anagwira ntchito, ndipo monga tinapangidwa mu chifanizo chake tinapangidwa kuti tizigwira ntchito. Kuyambira pachiyambi, tchimo lisanalowe padziko, munthu amagwira ntchito.

Mbuku la Rute, timaphunzira za Rute. Iye akuthawa chilala ndi apongozi ake komanso ndiosauka kwambiri. Akubwelera mdziko la Moabu chifukwa amva zoti kuli chakudya kumeneko. Lute akupeza ntchito yogwira kumunda wa Boaz, yemwe akuchita naye chidwi ndipo akudziwa zomwe wachitira kwa apongozi ake..

- Kodi Boazi anatani pofuna kuthandiza Lute? (Rute 2:15-16)
- Kodi mukuganiza kuti mchifukwa chiyani sanangomupatsa tirigu?

- *Chifukwa choti tinapangidwa kuti tigwire ntchito, Chifukwa timapeza ulemu kusiyana ndikungokhala olandira za ntchito zachifundo. Pochita izi, Boaz anapeleka ulemu kwa Rute.*

Zomwe Baibulo limakamba Zokhudzana ndi Ntchito

MAGULU ANG'ONOANG'ONO

Pogwiritsa ntchito Handout 4.1 kambiranani. Kodi zifukwa zina zogwilira ntchito ndichani? Gwiritsani ntchito Mavesi otsatirawa ndi maganizo ena omwe muli nao mu phunziro ili.

- 1 Atesalonika 4:11-12
- 1 Timoteo 5:8
- Aefeso 4:28
- 1Akorinto 10:31

ZOKAMBILANA GULU LALIKULU

- Kodi mukuganiza kuti Mulungu akufuna kuti tigwire ntchito?
- Kodi anthu ntchito amaiona motani?
- Pamene Mulungu amadzala munda, kapena Yesu anali okhoma matabwa, kodi mukuganiza kuti ntchito imeneyi amaiona bwanji?
- Kodi tingakhale bwanji ndi makhalidwe ofanana ndi Mulungu?
- Kodi tingathandize bwanji ena kukhala ndi makhalidwe ofanana ndi Mulungu pantchito yao?

ALIYENSE PAYEKHA

- Kodi mumaiona bwanji ntchito?
- Kodi mukufunika kusintha maganizo anu momwe mumaionera ntchito?

Pempherani kuti Mulungu akuthandizeni kuona ntchito yanu monga lye amaionera ndipo izi zidzakuthandizani kukhala ndi chikhalidwe ngati lye.

Mitundu ya Ntchito

ZOKAMBILANA GULU LALIKULU

- Mukuganiza kuti mitundu ina yanthito ndiyopambana kusiyana ndiina? Kodi chimaipangitsa kukhala yopambana ndichani?

MAGULU ANG'OANG'ONO

- Kodi Mulungu anapeleka ntchito yotani kwa Adamu?

- Kodi Mulungu anapeleka ntchito yotani kwa Nowa?
- Kodi Mulungu anapeleka ntchito yotani kwa Yosefe?
- Kodi Mulungu anapeleka ntchito yotani kwa Danieli?
- Kodi Mulungu anapeleka ntchito yotani kwa Gidiyoni?
- Kodi Mulungu anapeleka ntchito yotani kwa Mose?
- Kodi Mulungu anapeleka ntchito yotani kwa Davite?
- Kodi mukuganiza kuti Mulungu akanakonda kuti anthu awa atsogolere mpingo kapena kulalika pamapemphero mmalo mogwira ntchito yomwe anawapatsa?
- Mukuganiza kuti Mulunguanawelengera anthu apansi kusiyana ndi ansembe? Mwachitsanzo, ntchito ya Mose inali yotsika kusiyana ndi ya Aroni?

Ganizo loti ntchito zina ndizotsika kusiyana ndi zina silipezeka mbaibulo. Iyi inali ganizo lachikhalidwe cha chigriki lomwe linali gawo loyamba la kuganiza kwa akhristu mpaka nthawi ya kusintha (lifomu). Agriki ankakhulupilira kuti mizimu ndiyapamwamba komanso yolemekeza Mulungu pamene zinthu ndizotsika ndipo zosafunikira kwa Mulungu.

Komatu iyi sinkhani ya mbaibulo. Baibulo imayamba ndi kulengedwa kwa dziko ndi Mulungu. Pa Genesis 2:8 tikuona Mulungu akudzala munda. Mulungu yemwe timamupembedza ndi kumupatsa ulemu, anadzala munda. Pamene tikugwira ntchito zakumunda, tiyeni tikumbukire kuti Mulungu anali oyamba kudzala. Tikupanga zomwe Mulungu Anapanga zaka zapitazo. Kawirikawiri Mulungu akuitana anthu kuti amutumikire munjira zosiyanasiyana. Pamene kukhala Mlaliki ndi ntchito yolemekezeka, chimodzimidzi ulimi, kukhoma matabwa, kapena uphunzitsi. Sitikungofunika kuti anthu atiphunzitse zauzimu, komanso kudzala chakudya choti tidye, kumanga nyumba yokhalamo, ndikuphunzitsa ana athu. Mkhristu wina otchuka, John Wesley yemwe anakhalapo zaka mazana apitawo anapeleka malangizo otsatirawa okhudzana ndi ntchito.

Malangizo a John Wesley (Visual Aid 2)

- Ntchito siikuyenera kuononga thanzi/umoyo lanu.
- Ntchito siikuyenera kuononga banja lanu.
- Ntchito siikuyenera kutsutsana ndi chikumbumtima chanu.
- Ntchito siikuyenera kukhumudwitsa oyandikana nao kapena kusokoneza kapezedwe kao kandalama.
- Ntchito siikuyenera kuononga thupi la amene mwayandikana nao.
- Ntchito siikuyenera kuchimwitsa oyandikana nao.

John Wesley anati pambali pakugwiritsa ntchito malangizowa tikuyenera kugwiritsa ntchito maluso athu pogwira ntchito molimbika. Tikuyenera kulimbikira kuti tipeze zokwanira kuti tikwanilitse kuyang'anira banja lathu, kusunga zamtsogolo, kupeleka Zothandizira kutukula ntchito ya Mulungu ndikupeleka kwa osowa. Munjira imeneyi tikulemekeza Mulungu Pogwiritsa ntchito maluso athu, mphamvu ndi thanzi lomwe watipatsa.

ZOKAMBILANA GULU LALIKULU

Taonani malangizo a John Wesley

- Kodi chitsanzo cha momwe langizo lilonse lingafotokozedwe motani?
 - *Ntchito siikuyenera kuononga thanzi/umoyo lanu—kugwira ntchito malo oopsa, ntchito yosagwilizana ndikuthekera kwanu Mwachitsanzo ntchito yofuna mphamvu kwa munthu wachikulire.*
 - *Ntchito siikuyenera kuononga banja lanu— kugwira ntchito maola ambiri mpaka kuiwala banja lanu. Ntchito zofuna kuti mukhale kutari ndi banja lanu nthawi yambiri pamwezi mmalo mosamalira banja lanu.*
 - *Ntchito siikuyenera kutsutsana ndi chikumbumtima chanu— kuba kapena kutengerapo mwayi pamunthu wina.*
 - *Ntchito siikuyenera kukhumudwitsa oyandikana nao kapena kusokoneza kapezedwe kao kandalama— kuyamba bizinezi pafupi ndimunthu wina koma kugulitsa mtengo otsika kuti tipeze makasitomala (ogula) ake onse.*
 - *Ntchito siikuyenera kuononga thupi la amene mwayandikana nao— kufuula mowa kapena kupanga fodya*
 - *Ntchito siikuyenera kuchimwitsa oyandikana nao— kuyendetsa bizinezi ya malo omwera mowa (bala).*
- Ngati timakhulupilira kuti ntchito iliyonse imalemekeza Mulungu ndiye zimenezi zimakhudza mmene timaonera ntchito yathu.
- Kodi izi zimakhudza bwanji mmene mumagwilira ntchito?

Mulungu Amasamala Mmene Timagwilira Ntchito

Nthawi zambiri zimanenedwa kuti ogwira ntchito achikhristusagwira bwino ntchito.

- Mukuganiza kuti mchifukwa chiyani izi zitha kukhala zoona?
- Kodi zimachitika mdera lanu?
- Kodi mukuganiza kuti Mulungu amamva bwanji ndi akhristu amchitidwe umenewu?

Pamene Baibulo silinenakuti ntchito zina ndizofunika kuposa zinzake, Baibulo imayankhula zambiri za momwe tikuyenera kugwilira ntchito. Ntchito ndimbali yofunika kwambiri Chifukwa timaononga nthawi yathu yogona kugwira ntchito, ndiye tikuyenera kusamala ndi mmene timagwilira ntchito.

MMAGULU ANG'ONOANG'ONO

Onani Mavesi otsatirawa. Kodi mavesiwa akutiphunzitsa zotani? Mmagulu kambilanani ndikulemba ndime imodzi mwachidule.

- 2 Atesalonika 3:10-12
- Miyambo 10:4

- Miyambo 19:15
- Miyambo 21:25

Kodi mukuganiza kuti mavesiwa akuphunzitsa chiyani pa momwe tingagwilire ntchito?

- 1 Akorinto 10:31 –Lemekezani Mulungu
- Akolose 3:23- Gwilani ntchito ngati mukugwilira Mulungu

ZOKAMBILANA GULU LALIKULU

Nthawi yaitali Yesu anali okhoma matabwa. Tangoganizani kuti mukanamuona lye nati okhoma matabwa.

- Kodi mukuganiza kuti ntchito yakeinali yooneka motani? ?
- Tangoganizani kuti munagwilapo ntchito malo amodzi ndi Yesu: zikanakhala bwanji kugwira ntchito ndi Yesu malo amodzi ogwilira ntchito?
- Kodi mukuganiza kuti iyeyo akanaonetsa khalidwe lotani
- Kodi iyeyo akanatani pomwe wina sakugwira ntchito?

Nthawi ya kusintha (lifomu) , kusintha kwakukulu kumachitika pakagwilidwe ntchito ka akhristu. Kwa nthawi yoyamba anthu anayamba kuwerenga Baibulo kuti aone mmene imagwilira ntchito mmoyo wao wa tsiku ndi tsiku. Nthawi imeneyo, ngati okhoma matabwa wakonza tebulo, amaonetsetsa kuti pansi pa tebulo ndipooneka bwino chimodzimodzi mwamba mwake. Amati Mulungu atha kuona pansi patebulo mosavuta ngati pamwamba, ndipo okhoma matabwa amagwira ntchito kuti akondweretse Mulungu. Zipangizo zopangira nthawi imeneyo zidali zapamwamba kwambiri mkale lonse.

MMAGULU ANG'ONOANG'ONO

Sewero

Sankhani ntchito ndipo mupange masewero awiri: yoyamba yoonetsa munthu akugwira ntchito munjira yokondweretsa Mulungu, ndi ina yoonetsa munthu ogwira ntchito osakondweretsa Mulungu. Pangani kuti gulu lonse lionse.

GULU LALIKULU

Pakutha pa sewero lililonse kambalanani:

- Ndi njira zotani zomwe mwazona munthu ochita sewero akudzetsa ulemelero kwa Mulungu muntchito yake?
- Ndi njira ziti zomwe mwazona kuti munthu ochita sewero sakudzetsa ulemelero kwa Mulungu muntchito yake?
- Kodi maganizo ena omwe tingaonjezere ku ndandandawu ndiotani?

ZOLINGALIRA PAYEKHAPAYEKHA

Talingalirani za ntchito yanu. Kodi ndinjira zotani mumalemekeza nazo Mulungu pantchito yanu?
Mufunсени kuti akuonetseleni zinthu zomwe mutha kupanga kuti mumulemekeze bwino kuposa mmene mukuchitira.

Phunziro 5: Kumanga Ufumu wa Mulungu

Zolinga

- Tikuyenera kukhala omvera pamoyo wathu ndi wapabanja lathu kuti tisinthe madera athu kuti afanane ndi Ufumu wa Mulungu.

Zipangizo

- Handout 5.1 ‘Banja Limodzi Lachikhristu Limadzetsa Kusintha kwa Nkhani
- Handout 5.2 Kodi Mungakhale Bwanji Omanga Ufumu
- Posita – Kuchokera kwa Munthu Payekha Mpaka pa Banja

Zimayamba ndi lfe

Mu phunziro limodzi takamba za momwe Mulungu watipatsira masomphenya apamwamba.

- Kodi masomphenya ake ndiotani?
 - *Ufumu wa Mulungu*
- Kodi tingatani kuti tiyambe kukwanilitsa masomphenyawa?

Dera Losinthika

Werengani nkhanu yotsatirayi.

Dera lina, akhristu akhala akudziwika kuti ndi osauka kwa zaka zambiri. Mabanja ambiri amkapeza ndalama zochepa. Iwo amakakamizika kukalima minda yakutali ndi komwe amakhala, ndipo amayenera kunyamula zokolera zao pamutu chifukwamiseu inali yoonongeka kotero kuyenda pagalimoto kunali kosatheka. Mabanja ambiri anali ndi mpunga okwanira kuchokera nthawi yomwe akolera chaka chonse kufikira mwezi wa chisanu ndi chimodzi (6). Mbali ina yachaka amasaka mtchire kuti apeze chakudya. Chifukwa choti samadziwa kusamalidwe ka ndalama zao, chaka chilichonse Mabanja akumeneku amakhala ndi ngongole. Deralo linalibe zimbudzi, ndipo anthu amadwala pafupipafupi. Nyumba zao zinali zazing’ono komanso zodontha. Ana amdelari Kawirikawiri samapita ku sukulu. Mpingo unali waung’ono ndipo osauka amakumana ndi mavuto aadzaoneni chifukwa cha kutonzedwa komanso kugawanikana kwa anthu a mderali.

Mabungwe achitukuko samaloledwa kugwira ntchito ndi anthu a mderali, ndipo panali chiyemebekezo chochepa kuti anthu angachoke mu msampha waumphawi. Koma izi zinasintha pomwe banja lina linabwera ndikuyamba kuphunzitsa atsogoleri ammipingo amderali pa momwe angakondere anthu

oyandikana nao, komanso pa zomwe Ufumu wa Mulungu umatanthauza. Iwo sanapereke ndalama kumipingo, koma anangowaphunzitsa kumvera malamulo a Mulungu.

Mmipingo inalandira uthengawu pothandiza anthu ena mdera lao. Anakonza ndi kukulitsa miseu. Anathandizana kukolola. Anamanga ndikukonzanso nyumba zao. Anamanga zimbudzi. Anatumiza ana awo ku sukulu. Anayamba kupatsana ulemu mmabanja awo.

Pakutha pa zaka zisanu zokha derail linasintha kwathunthu. Atsogoleri amderali anabwera kudzafofotokozeka ku banja linawaphunzitsa lija kuti siosaukanso ayi. Ndalama zomwe amkapeza zakwera. Anali athanzi. Ana awo amapita ku sukulu. Komanso mpingo unakula. Pafupifupi aliyense mderali anasintha mkukhala khristu poona mmene mpingo ukuonetsera chikondi mderali. Mpingo unali ndi ubwenzi wabwino adindo amderali, ndipo chitonzo chinatha.

Pamene gulu la ogwira ntchito zachitukuko lachikhristu linadza kudzaona zomwe zachitika kuderali, sanakhulupilire kuti derail linali losauka zaka zisanu zapitazo. Iwo atazindikira za kusintha komwe kunachitikakwanthawi yochepa anali odabwa! Anayamba kufunsa mtsogoleri aliyense, “Kodi munapanga chiyani kuti mudzetse kusintha kwa mtundu otere?”

Mukudziwa zomwe atsogoleri anayankhula? Aliyense amayankha kuti: “Tinali omvera Mulungu.”

ZOKAMBILANA GULU LALIKULU

- Kodi chidadzetsa kusintha ndi chiyani mderali?
- Kodi ndizauzimu kapena zakuthupi?
- Mmene ogwira ntchito yachitukuko anafunsa za chomwe chadzetsa kusintha, amayembekezera yankho lotani?
- Kodi yankho yomwe aliyense anawauza inali yotani?
- Kodi mipingo ya mderali inachita chiyani mdera lao pofuna kuonetsetsa kuti ikumvera Mulungu?

Kodi Tingadzetse Bwanji Kusintha Mdera Lathu?

Ngati tikufuna kusintha mdera lathu tikuyenera kumvera Mulungu. Njira yoyamba ndikusintha moyo wathu. Tikuyenera kuyamba kugwiritsa ntchito mfundo zoyenera muufumu pamoyo wathu ndi zochitika zathu zonse.

ZOKAMBILANA GULU LALIKULU

- Kodi miyoyo yathu ikanakhala motani tikanakhala kuti timamvera chifuno cha Mulungu tsiku lililonse?
- Ganizani zinthu zowerengeka za mmene tsiku lanulimakhala. Akanati mumamvera Mulungu muzonse, mukanapanga zimenezi? Mukanazipanga mosiyana?
- Kodi chifuniro cha Mulungu chimakhudza motani zinthu monga kugona, kudya, kukonza chakudya, kudza kumunda kapena kutunga madzi? Kodi Mulungu Amasamala mmene timapangira ntchito zimenezi?

- Werengani Mateyu 6:25-33
 - Kodi anthu amakhala ndi nkhowa chifukwa chiyani? Kodi ndizauzimu kapena zinthu wamba?
 - Kodi Yesu anayankha motani?
 - Kodi mukuganiza kuti Yesu amatanthauza chiyani? Kodi tingafune bwanji Ufumu wa Mulungu muzonse?

Zitha kukhala zodabwitsa kuganiza kuti anthu anadza kwa Yesu kumuuza kuti anali ndi nkhowa ya yoti adzadya ndikumwa chiyani, ndipo yankho lake linali loti “yambani mwafuna Ufumu wa Mulungu.” Kodi izi zikutanthauza chiyani? Kodi zikutanthauza kuti tisaganize zinthu izi, koma nthawi zonse kupanga zauzimu monga kupemphera? Ngati tingapange ndie kuti ungakhale moyo opanda banga?

Mwamwayi winawake yemwe anakhala moyo opanda banga ndikuchita chifuniro cha Mulungu nthawi zonse: Yesu (Yohane 14:31). Titha kuona za moyo wake kuti tione tanthauzo la kufuna Ufumu wa Mulungu choyamba. Taonani Mavesi awa. Akutiphunzitsa chiyani pa zinthu zina zomwe Yesu anapanga?

- Marko 6:3 – mpaka zaka makumi atatu Yesu anali okhoma matabwa. Mdera lake samadziwika ngati mtsogoleri wauzimu wamphamvu, koma munthu wamba. Pamene Yesu anali okhoma matabwa lye amakhala moyo opanda banga (osachimwa). Panalibe nthawi mmoyo wake pomwe anachita zotsemphana ndi chifuniro chamulungu. Kuyambira zaka khumu mpaka makumi atatu, chifuniro cha Mulungu pa Yesu chinali choti atsate zomwe banja lake likupanga ndikukhala okhoma matabwa. .
- Yohane 21:9-14 – Yesu anaphikira chakudya ophunzira ake.
- Marko 4:38 – lye atatopa anapuma.
- Yohane 2:1-2 – Yesu amapita kuukwati.
- Kodi izi zinali zinthu wamba kapena zauzimu?
 - Zinali zinthu wambangakhale zinali zinthu zomwe Yesu amapanga patsiku. Pamene amafuna Ufumu wa Mulungu nthawi zonse, amapanga zinthu zawamba patsiku. Nthawi iyisikuti anali kunja kwa chifuniro cha Mulungu, koma amatumikira Mulungu kwathunthu.

Werengani Marko 1:21-34.

- Kodi zina mwa ntchito zomwe Yesu anachita patsiku ili zinali zotani?

Mmavesi awa tikuona sabata mmoyo wa Yesu. Mammawa anali ku sunagoge kuphunzitsa. Kenako amapita kunyumba ya Peturo, ndiye atatha kuchiza Mayi ake, anapuma pamene Mayi a Peturo anawatumikira. Usiku lye amapita kukatumikira anthu ena pakuchiritisa odwala.

- Kodi izi zikusiyana bwanji ndi mmene timakhalira tsiku lathu Lamulungu? Kodi pali kusiyana kotani, ndipo pali kufanana kotani?

Monga tikuonera, zaka zoyambilira za moyo wake, Yesu anali okhoma matabwa. Ngakhale anayamba kuphunzitsa ena, sikuti nthawi zonse amapemphera ndikuphunzitsa. Amadya ndi anzake, amatumikira anzake, amagona komanso amapuma. Zonse zomwe anachita zinali zoyenera malingana ndi chifuniro

cha Mulungu. Ngakhale akamachita zinthu zawamba, amachita zomwe Mulungu amafuna kuti iye achite.

M'bale Lawrence

Mchaka cha 1608 munthu wina anabadwa mdziko la France. Iye anakhala mkristu ali ndi zaka khumi zisanu ndizitatu (18), ndipo ali mu zaka za makumi awiri (mma 20) amaganiza zodzipereka kutumikira Mulungu kwathunthu. Iye analowa gulu la anthu odzipereka kutumikira Mulungu (Monastery) komwe anapatsidwa dzina loti M'bale Lawrence. Anaganiza kuti kukhala monasitele kuthandiza kuti adzikhala malo opembedzera kupemphera ndikulemekeza Mulungu nthawi zonse. Mmalowo mwake, iye anapatsidwa ntchito ya kukhitchini. Kwa zaka khumi amadana ndikukhala kukhitchini pomwe ena anali kumalo opembedzera. Anadana ndikupatsidwa ntchito yosafunikirayi.

ZOKAMBILANA GULU LALING'ONO

- Mukanakumana ndi Mbale Lawrence zaka khumi zoyambirazi, mukanawapatsa malangizo otani?
- Mukuganiza kuti ntchito ya M'bale Lawrence yakukhitchini inali yosafunikira kusiyana ndi ena omwe anali ku malo opembedzera?
- Werengani Mavesi otsatirawa ndipo ganizani momwe mungawagwilitsire ntchito ku nkhani ngati imeneyi:
 - Mateyu 25:40 (34-40)
 - 1 Akorinto 10:31
 - 1 Akorinto 13:1-3

Pakukha pa zaka khumi M'bale Lawrence anazindikira kuti atha kutumikira ndikupembedza Mulungu posatengera komwe ali. Iye anapitiliza kukhala ku khitchini, koma anayamba kumva kuti anali ndi Mulungu ngati akutumikira malo opembedzera.

Baibulo ikutionetsa kuti Mulungu ndiokhudzika ndi momwe timapangira zinthu zomwe timapanga, ngati zomwe tikuchita sitikuchimwa. Chilichonse chomwe tikupanga chitha kugwiritsidwa ntchito kudzetsa ulemelero kwa Mulungu.

Kuchokera kwa Munthu Payekha Kupita pa Banja ndi ku Madera

Kusintha kumayamba ndi munthu payekha ndikupita pa banja, kenako kudera ndi dziko lonse. Iyi ndi dongosolo. Pamene anthu paokha akumvera Mulungu, zimakhudza madera awo. Pamene madera ayambe kumvera Mulungu, zimakhudza madera ena ozungulira, mpaka dziko lonse.

Mabanja

Werengani mavesi otsatirawa:

- Deuteronomo 6:7
- Tito 2:3-4
- 1 Timoteo 3:12
- Tito 1:6
- Kodi tikuyenera kusintha motani mabanja athu?
 - *Tikuyenera kuphunzitsa ndikuonetsa chitsanzo chabwino kwa iwo.*

Werengani Luka 2:52

- Kodi ndi phunziro lotani lomwe mwalipeza pa vesi ili mmaphunziro a mbuyomo?
 - *Tikuyenera kukula mmagawo anayi.*

MAGULU ANG'ONOANG'ONO

Perekani njira zosiyanasiyana za momwe mungathandizire banja lanu kukula muzigawo zinayi. Kodi aliyense wasankha chinthu chimodzi chomwe apange (ubwenzi ndi ena, zauzimu, zakuthupi, zothandiza malingaliro)sabata ino.

Madera

Pamene mabanja akusinthika amakhala ndi chikhumbo choona madera awo akusinthika. Werengani nkhani iyi ya Bambo ena ndi banja lao lomwe linasintha dera. (kwa makalasi okutha kuwerenga perekani handout 5.1 ndipo funsani mafunso kwa ophunzira, aliyense Payekha).

Iyi ndi nkhani yeniyeni ya Bambo ena omwe anayenda ndi banja lao kupita kudera lina komwe kunalibe akhristu oti mkufalitsa za mkristu mderali. Iye amafuna ataona Ufumu wa Mulungu utamangidwa ndipo miyoyo ya anthu itapangidwanso mzigawo zonse – uzimu, kulumikizana ndi ena, zokhudzana ndi kaganizidwe ndi kuthupi.

Mkhristu Mmodzi Adzetsa Kusintha

Zaka zinayi zapitazo pomwe Mlaliki wina amapita ku dera la chi Hindu ili. Mudziwu unali kumapiri a Himalaya pamtunda wa mafiti 1, 000 makilomita ochepa panali Esiteti ya tiyi. Anthu ambiri a mmudziwu amkapeza ntchito kumeneku. Komabe, malipiro ake anali ochepa choncho anthu amavutika kuti akhale bwino ngakhale anali pantchito.

Mudziwu unali ndi nyumba pafupifupi makumi awiri ndi zisanu zinali zosalongosoka, zomangidwa ndi mitengo ndipo madenga ake anali a zitini. Munalibe zimbudzi mmudzimo. Chifukwa choti unali malo okwera kumkazizira kwambiri; komabe ana amayenda popanda nsapato ndiponso anali onyentchera.

Nyumba iliyonse inali pakachisutswa cha munda. Chakudya chimaphikidwa malo ena aang'ono odzazidwa ndi utsi, ndipo poto amakhala pa miyala itatu. Panali nkhuu zochepa zomwe zimalowa ndikutuluka nyumba ndipo malo ozungulira anali auntchisi.

Sukulu yapafupi inali pamtunda wa makilomita awiri. Mtundawu unali wautali kuti ana adziyenda tsiku lililonse ndipo amkafunika kugwira ntchito zina zapakhomo. Chifukwa cha ichi ana ambiri samapita ku sukulu. Akuluakulu ambiri samadziwa kulemba ndi kuwerenga, choncho amadyeledwa masuku pamutu ndi anthuena ochokera kumidzi ina komwe amatha kulemba ndi kuwerenga.

Kunali malo ochepa olima chifukwa madzi apafupi amapezeka pamalo ena osungira madzi omwe anali pa mtunda wamakilomita awiri. Zinali zovuta kuti apeze madzi okumwa ndi osamba, koma ongothilira madimba. Kanthawi kena panali paipi yodutsira madzi kuchokera ku malo osungira madzi, koma siimagwira ntchito ndipo anthu sanapange chilichonse kufuna kuibwezeletsa.

Mvula inali yosakhazikika kupatula nthawi imodzi pamene kumakhala mvula yokwanira kudzala mbeu yodalirika ya mpunga. Panalibe nthawi yokwanira kudzera masamba. Ngati ali ndi mwayi amatha kukolora mpunga okwanira omwe umawafikitsa chaka china nthawi yokolora.

Anthu anali a mtundu wa Hindu, choncho amkapembedza milungu yosiyanasiyana. Kuli milungu yopitilira miliyoni imodzi, yomwe anthu a chi Hindu amachita nayo bata ndikuipembedza. Mudziwo unali ndi mafano ang'onoang'ono ambiri a milungu ya a Hindu. Nthawi iliyonse yomwe munthu wadya chakudya amataya china pansi kwa mizimu yoyendayenda.

Anthu analibe ndi mtima oonetsa kugonja ndi kusowa chiyembekezo. Chiyembekezo chokha chomwe anali nacho chinali pamoyo wina womwe adzakonzedwenso zinthu ndi kukhala bwino. Komanso panali mpata wina ngati sanakondweretse milungu, atha kupangidwa ngati khoswe kapena galu. Iwo amkamva ngati akodwa mu (khwekhwe) msampha, popanda njira yosinthira miyoyoyao.

Lepcha anali Mlaliki yemwe anasamukira kumalowa. Iye anaphunzira maphunziro a maziko a kuthandiza thanzi la anthu kwa mwezi umodzi. Atamaliza maphunzirowa anapita ndi banja lakekukakhala kumudzi kuja kuti athandizane ndi oyandikana nao nyumba pogawana naozomwe anaphunzira. Anali ndi bwalo laukhondo ndi malo ophikira omwe anali pamtunda zomwe zimapangitsa kuti asavutike pophika komanso agwiritse ntchito nkhuu zochepa. Anali ndi kanyumba kosungira nkhuu. Analima dimba laling'ono la masamba, yomwe inasintha thanzi la ana awo. Anali ndi chimbudzi panja ndipo ana awo samadwala matenda otsekula mmimba ngati ana ena a mmudziwo.

Lepcha anakonza chida chosungira madzi a mvula okugwa kuchokera padenga la nyumba yake pomwe mvula yosakhazikika imadza. Anthu ena anatengera nao nzeruyi, nao anayamba kukhala ndi madzi.

Iwo anathandiza anthu a mmudziwo kuti azigwira ntchito pamodzi ndipo anaika paipi yodutsira madzi kuchoka mmalo osungira kukafika kumudzi, ndipo anthu ndi madzi okwanira, okwanira kuthilira minda yao ya masamba. Anthu ambiri anatengera chitsanzo cha nyumba ya nkhuu ndipo Anamanga zimbudzi zopanda fungo komanso ntchentche.

Pomwe banja la Lepcha's inabwera inayamba kuphunzitsa akulu ndi ana omwe amafuna kuphunzira kuwerenga ndi kulemba. Lero, mudziwu muli sukulu ya ana kufikira kalasi ya chinayi.

Lero kuli tchalitchi yaing'ono chifukwa kuli mabanja makumi awiri ndi atatu (23) mwa mabanja makumi awiri ndi asanu (25) omwe ali paubwenzi ndi Mkhristu. Zonsezi chifukwa cha banja limodzi lomwe linagawana ndi anthu za Mkhristu ndi mau awo komanso ntchito zao.

Anthu amkamva kuti akanilitsa chinachake, ndipo anaona kuti atha kukhala miyoyo yathanzi chifukwa banja limodzi linabwera ndi kugawana ndi ena.

Nkhani iyi imakambidwa kawirikawirimidzi ya kumpoto kwa India ndi kummawa kwa Nepal. Lero zinthu ngati izi zikuchitika midzi zana limodzi ndi makumi awiri ya kuderali. Miyoyo ya anthu yasinthika kuthupi. Koma anthu a mmudziwu asinthika kuuzimu ndipomikumano yachikhristu 107 yayambika, ndipo mikumano yaikulu 12 ili ndi mamembala 200.

Azibusa a ku India anayambitsa mpingo wao otchedwa Agape, omwe anthu ambiri akulowa. Pomwe banja limodzi ngati la Lepcha, ili ndi masomphenya kuti ione dera lao litasinthika, zazikulu zimachitika mwa Mulungu ngati akufuna chifuniro cha Mulungu ndipo ndi ololera kutsatira masomphenya omwe Mulungu awapatsira. Ena mwa zitsanzo zabwino za mmabanja anasinthika kukhala zitsanzo za mu mpingo kudzera pa kuphunzitsa anthuodziwika mu mpingo. Ndi pemphero lathu kuti kutsogoloku adzakhale zitsanzo za dera lonse.

- Kodi kusintha komwe anabweletsa Lepcha mkotani? Taonaninso nkhani ya Lepcha ndikulemba ndandanda wa zinthu pansi pa ubwenzi ndianthu ena, zauzimu, zokhudza maganizo ndi kuthupi.
- Kodi iye anabweletsa kusintha motani? Anayamba ndindani? Naja lake.
- Kodi derail linasinthika bwanji chifukwa cha Lepcha?
- Kodi mungakhale bwanji ngati Lepcha mdera lanu?

Zoyenera kudziwa: *Gawo lachinayi tibweletsanso maphunziro a zaumoyo ofanana ndi omwe Lepcha anaphunzira.*

Zitsanzo za Anthu ena Omwe Anamanga Ufumu wa Mulungu

Werengani nkhani zotsatirazi, kukambirana Mafunso pakutha pa nkhani iliyonse.

Kupita ku Zipatala

Mbusa wina mdziko lina amkagawa mabuku pa mizikiti. Boma inali siinakondwere ndiizi ndipo inalanda zikalata zochitira utumiki wake. Tsiku lina anatenga nao gawo pa maphunziro ndipo anaphunzira za momwe angaonetsetse chikondi cha Mulungu kudzera pakuonetsa chikondi. Anaganiza za ganizo lina latsopano. Iye anatenga anthu ogwira ntchito modzipereka, anagula buledi ndipo anapempha oyang'anira chipatala cha mderalo kuti adzikaona odwala, kugawana nao buledi ndi kuwapemphelera. Iwo analandira chilolezo, koma anapatsidwa mawadi ovuta: otsekedwa komwe kumakhala odwala nthenda ina yosachilitsika ya schizophrenic. Mmodzi mwa odwalao anali mwamuna yemwe sanalankhulepo kwa zaka zambiri. Mmalo moyenda iye amakwawa. Nkhope yake inali yotupa ndiponso yokandikakandika. Limodzi mwa makutu ake linali lalikulu kwambiri. Amatulutsa fungo lonunkha.

Ankangokhala osadzikonza. Alendo anaika manja pamutu wake ndikupemphera ndipo sanafune kugwira chilichonse mpaka atasamba.

Sabata lotsatira, Abusa ndi ogwira ntchito modzipereka aja anabweranso. Anakumana ndi munthu ochepa thupi wamtali yemwe anali wadi ya ovutika maganizo (amisala). Anamufunsa kuti awatengere ku gulu la odwala kwambiri. Iye anawauza kuti ndi yemwe anamupemphelera sabata lapitalo – mapemphero awo anamusintha ndipo amkafuna kuti amupemphelerenso. Ngakhale Zinali choncho, gulu lija silinamuzindikire, ndiye anamuuzza kuti alibe nthawi yokwana koma amafuna awatengere ku komwe kunali odwala ena. Iye ndi ogwira ntchito mu wadiyo anatsimikiza kuti munthu wake ndi yemweyo yemwe anamupemphelera sabata lapitalo. Gulu lotumukira inali yodabwa. Munthu uja anachiritsidwa. Anayenda ndipo anayamba kulankhula. Amathanso kulemba. Nthenda yake inachoka pa yosachilitsika kukhala yochilitsika.

Mukupita kwa nthawi, otumikira aja anapitilira kupita ku chipatala kuja komwe amapita ndi buledi ndi zovala komanso kupemphelera odwala. Odwala enanso anayamba kusintha. Kenako, gulu lija linauzidwa kuti litumikire odwala onse 800 ndi ogwira ntchito pachipatalapo. Mulungu anawathandiza pochulukitsa zipangizo zao pomwe anthu ena anamva za ntchito yomwe akugwira. Pakutha pa zaka zitatu ndi madalitso a atsogoleri a derail, gulu lalikulu limatumikira sabata lililonse kwa anthu 2600 mzipatala zisanu, malo okhala ana amasiye, ndende ziwiri ndi malo omwe anthu okumwa mankwala osokoneza bongo amathandizidwa. Anayamba kutumikira kwa ana oyenda mmiseu ndi osowa malo okhala.

- Kodi chinachitika mu nkhani iyi ndichani?
- Chinayambitsa ndi chani?
- Iye Anapanga chiyani?
- Zotsatira zake Zinali zotani?
- Kodi dera lake linali ngati momwe Mulungu amafunira malingana ndintchito zake?
- Kodi tingaphunzire zotani kuchokeraku nkhani iyi?

Kuchokera pa Ozunzidwa Mkukhala Otsogolera

Panali Abusa ena mdziko lina omwe amaitanidwa pafupipafupi ku Polisi. Pafupifupi kasanu ndi kamodzi (6) pachaka Apolisi amabwera ku malo omwe amachititsira maphunziro ndikumutengera ku Polisi. Tsiku lina anaphunzira za kumanga Ufumu wa Mulungu ndipo anayamba kuphunzitsa izi ku mpingo wake. Analimbikitsa mpingo wake ndi omwe amawatumikira kuti ayambe kutumikira anthu oyandikana nao ndikusaka mwayiopanga dera lao kukhala monga momwe Mulungu akanafunira kuti ikhale.

Mipingo inayamba kuchita ma pulojekiti osiyanasiyana: kupeleka kwa osowa, kumanga nyumba kwa akazi amasiye, kukonza miseu, kumanga zimbudzi ndi zina. Mpingo unayamba kukula ndipo okhulupilira anakula mu nzeru. Makhaliidwe oipa monga kumwa mowa ndi juga zinatha mderali. Pagonopangono adindo a Boma anadziwa za kusintha komwe Mbusa ndi mipingo anadzetsa mderalo. Zotsatira zake anamupanga Mbusa uja kukhala mdindo wa Boma oyang'anira dera lija. Anayamba udindo wake pophunzitsa omwe anali pansi pake maphunziro a zaumoyo kuti akwanitse kuphunzitsa aliyense mderalo. Thanzi la anthu okhala mderalo linayamba kusintha.

- Kodi Mbusa anapanga chiyani?
- Kodi iye akumanga Ufumu wa Mulungu mu njira zotani?
- Kodi zotsatira zake ndi zotani?
- Kodi tikupeza maphunziro otani mu nkhani iyi omwe tingawiritse ntchito pa miyoyo yathu?

Ana Kupita ku Sukulu

Dera lina chiwerengero cha ana opita ku sukulu ndi chochepa. Munthu wina pozindikira kufunikira kwa maphunziro anaganiza zochitapo kanthu. Analankhula ndi ena mu mpingo za vutoli ndipo anasonkhanitsa gulu la anthu omwe anali okonzeka kugwira naye ntchito pofuna kuthana ndi vutoli. Anayamba kuyenda khomo ndi khomo kulimbikitsa mabanja kutumiza ana awo ku sukulu. Zotsatira zake ana onse a mderalo anayamba kupita ku sukulu. Oyang'anira za maphunziro a mderali anadziwa zomwe zimachitika ndipo anamuitana kuti apite mmadera ena kukalimbikitsa makolo kutumiza ana awo ku sukulu. Pakadali pano, osati ana a mmudzi mwake okha amapita ku sukulu komanso midzi ina yozungulira.

- Kodi ndi njira zotani zomwe munthuyu akumanga Ufumu wa Mulungu?
- Kodi ndizotheka bwanji kupanga zofanana ndi izi mdera lanu?

Titha kukhala odzetsa kusintha mdera lathu. Anthu awa sanali apaderadera kapena odalitsidwa kwambiri. Anali anthu wamba ngati inu ndi ine. Ena anali ndi maphunziro ochepa koma anali lolera kupanga zomwe akanatha pofuna kumanga Ufumu wa Mulungu mdera lao.

Kodi Mungakhale Bwanji Omanga Ufumu

Mulungu atha kupanga chilichonse chomwe akufuna. Atha kumanga Ufumu wake popanda ife. Koma alibe ganizo limenelo; iye ali ndi ganizo lotigwiritsa ntchito kumanga Ufumu wake. Kumanga Ufumu wa Mulungu kumayamba ndi ife. Werengani kapena kugawa Handout 5.3. kwa ophunzira ndipo muwauze kuti apemphere momwe angayankhire Mafunso.

Gawani Handout 5.2 – Kodi tingakhale bwanji ufumu

- **Yambani nokha**

Njira yoyamba kuti tione Ufumu wa Mulungu utamangidwa mmoyo wathu, pabanja lathu, mu mpingo wathu, mdera lathu, ndi padziko ndi kudziunikira. Muli okonzeka kugwilitsidwa ntchito ndi Mulungu? Muli okonzeka kumvera Mulungu mbali zonse za moyo wanu? Kodi chinthu chimodzi kapena ziwiri zomwe mungafune kusintha pantchito yanu sabata ino?

Phunzitsani ndi kulimbikitsa banja lanu

Pamene mukuyamba kugwiritsa ntchito Ufumu wa Mulungu mbali zonse za moyo wanu mukuyenera kulimbikitsa banja lanu kuchita chimodzimodzi. Pomwe tikawerenga, tikuyenera kuphunzitsa mabanja athu nthawi zonse (Deut. 6:7) posatengera zomwe tikupanga. Pezani njira

zophunzitsira banja lanu zochita, kudzera pakucheza nao, ndikuyang'ana njira zowathandiza kuyamba kutumikira ena.

Kumbukilani zinthu zomwe munalonjeza kuchita pa phunziro lililonse mmagawo anayi kuti athandize banja lanu kukula.

Funsani Mulungu kuti akugwilitseni ntchito kusintha ena

Yambani kupemphera ndikumupempha Mulungu kuti akuthandizeni kusintha anthu ena. Funani mwayi. Pomwe mukuona anthu ovutika, funsani Mulungu kuti akuonetseni momwe mungathandizire anthu amenewo.

Mulungu ali ololera kutithandiza kumanga Ufumu wake. Iye adzationetsera nthawi yovomerezeka, njira yoyenera kuthandizira.

Tumikirani Ena

Yambani ntchito za chikondi ndikupeza njira zina zothandiza kutumikira ena. Ngakhale simukumva kuti mungakwanitse kupanga zambiri, mutha kugwilitsa ntchito maluso omwe Mulungu wakupatsirani kuti mutumikire. Pamene mukutumikira, mudzayamba kukula ndipo mudzapeza kuti mwayamba kupanga zambiri.

Phunziro 6: Udindo wa Mpingo Pomanga Ufumu wa Mulungu

Zolinga

- Kudziwa kuti mpingo ukuyenera kukhala maziko akusinthira dera kuti lioneke ngati Ufumu wa Mulungu
- Kudziwa kuti munthu aliyense mumpingo ndiofunikira ndipo akuyenera kutenga nao mbali pomanga Ufumu wa Mulungu munjira inayake

Zipangizo

- Magawo ena a makadi

Chiyambi

Phunziro lapitalo timaona mmene kusintha kumachitikira – mmene kumayambira ndi inu ndikupita pabanja lanu, dera kenako dziko lonse. Komabe, pali gawo lina lofunikira la dongosololi: mpingo.

Kuti masomphenya awa akwaniritsidwe, dongosolo la Mulungu ndiloti mpingo ukhale ndi udindo ofunikira kwambiri kugwira mu dongosolo lakusinthali.

Werengani Aefeso 1:22-23

- Kodi udindo wa mpingo ndi otani?
 - Kukwanilitsa ntchito ya Yesu

Werengani 3:10

- Kodi Mulungu akugwiritsa ntchito chiyani kupangitsa nzeru zake kuti zidziwike?
 - Mpingo

Mavesi awa, kawirikawiri ndiovuta kumvetsa koma amatikumbutsakuti Mulungu wapereka udindo wapadera ku mpingo pantchito yomanaga Ufumu wake. Mpingo ndilo thupi la Khristu. Ndi udindo wa mpingo kukwaniritsa ntchito ya Yesu, poyanjanitsa zinthu zonse.

- Kodi chingachitike ndichani ngati mpingo wanu utatseka? Anthu omwe sali akhristu a mdera lanu angadandaule? Mchifukwa chiyani?

Mpingo ukuyenera kukhala ndi zotsatira mdera kotero kuti anthu a mdera atha kukhumudwa kuona mpingo ukuchoka.

Tiyeni tilembe chithunzi chathu cha phunziro la mbuyomo munjira ina. Tiyeni tiyambe ndi Munthu Payekha, kenako Banja, Kenako Dera, ndipo kenako Dziko. (Lembani pabolodi.)

Udindo wa mpingo ndikuthandiza dongosolo ili. (Lembani mpingo.) Tikuyenera kuphunzitsa anthu paokha kuti asinthe mabanja awo, madera awo ndi zina. Tikuyeneranso kupeza njira zothandizila mabanja ndi madera kukhala mwachifuniro cha Mulungu.

Kutukula Anthu

Malangizo: Perekani makadi ndi zithunzi za ziwalo a thupi (Visual Aid X) kwa mamembala angapo.

- Kodi ndi ziwalo ziti zomwe zili zosafunikira, kapena zomwe zilibe ntchito?
- Kodi chiwalo laling'ono kwambiri ndi liti?
- Kodi zotsatira za kuchotsa chiwalo chaching'ono kwambiri ndi zotani?
- Ngati ziwalo zonse zitasiyanitsidwa, kodi thupi lingagwire ntchito yake?
- Perekani zitsanzo za momwe ziwalo zosiyanasiyana za mthupi zimafunira ziwalo zina
- Kodi thupi lingakhale bwanji ngati ziwalo zina zikusowa mthupi?
Auzeni mamembala kuti atule pansi makadi awo
- Kodi thupi lingakhale bwino tsopano?
- Kodi zotsatira za kusowa kwaziwalo mthupi kungakhale kotani?

Uzani kalasi kuti isankhe gawo lofunikira kwambiri ndipo like makadi enawo pansi.

- Kodi thupi ingathe kugwira ntchito tsopano? Mchifukwa chiyani, tilibe chiwalo chofunikira kwambiri?

1Akorinto 12:12-20

- Mu thupi lamunthu, chiwalo chilichonse ndichofunika. Mpingo ukuyenera kukhala ngati thupi – membala aliyense wa mpingo akuyenera kukhala ofunikira pomanga Ufumu wa Mulungu. Pasakhale mamembala ena osafunikira. Kodi membala aliyense wa thupi akugwira ntchito yofunikira? Kodi pali anthu ena, omwe atasiya kusunkhana nao, sipangakhale kusintha pakayendetsedwe ka mpingo ndi mautumiki a mpingo?
- Kodi ndi chiwerengero chotani cha mpingo chomwe chikutenga nao mbali? Kodi ndi chiwerengero chotani cha thupi chomwe sichikutenga nao mbali kapena kugwiritsidwa ntchito?
- Funsani chiwerengero cha ophunzira pafupifupi chiwerengero chimenecho kuti atule pansi makadi awo.
- Kodi thupi lathu likanakhala ndi chiwerengero ngati chimenecho chogwira ntchito kodi zikanakhala bwanji? Kodi izinso ndi chimodzimodzi ndi mpingo? Kodi mpingo ukanayenda bwino chiowerengero chokwera chikanatenga nao mbali?
- Kodi tingatani kuti tithane ndi vuto limeneri?

Mchifukwa Chiyani Aliyense Akuyenera Kukhala Otumikira?

Werengani Aefeso 2:10.

- Kodi tinapulumsidwa kuti tigwire ntchito yanji?
- Kodi anthu onse omwe apulumsidwa akuyenera kupanga ntchito zabwino kapena owerengeka?
- Kodi aliyense mumpingo wanu akupanga ntchito zabwino?

Werengani fanizo la matalenti (Mateyu 25:14-30)

- Pomwe mukuwerenga fanizo ilikodi mukuganiza kuti pali akhristu ena omwe sakuyenera kugwiritsa ntchitomatalenti awo kuti amangire Ufumu wa Mulungu?
- Kodi akhristu onse akugwiritsa ntchito matalenti (maluso) awo mokwana?
- Kodi tingathandize bwanji anthu ochuluka kuti agwiritse ntchito matalenti awo mokwanira pomanga Ufumu wa Mulungu?

Kuti timange Ufumu wa Mulungu TONSE tikuyenera kugwira ntchito pamodzi. Pamene munthu atha kumanga kagawo kochepa paufumu wa Mulungu, mpingo onse umayamba kukhala monga Mulungu akufunira muzonse zapamoyo wao ndikuthandiza ena kupanga chimodzimodzi, titha kumanga Ufumu wa Mulungu. Tangoganizani ngati aliyense pampingo wanu anadzipereka kuti chifuniro cha Mulungu chichitike pamoyo wao, mumpingo ndi mdera. Kodi izi zikanadzetsa kusintha kotani pa mpingo ndi dera?

Aefeso 4:11-12

- Kodi udindo wa atsogoleri ndiotani (atumwi, aneneri, alaliki, abusandi aphunzitsi)?
- Mmipingo yambiri amati 10 peresenti ya anthu imagwira 90 presententi ya ntchito. Kodi ndizoona bwanji izi? Tingazisinthe bwanji?
- Kodi tingathandize bwanji ena kuti akwanitse kutumikira?

Kwambiri zimanenedwa kuti omwe amaphunzira kwambiri ndi omwe akutumikira ena. Mdziko la Indonesia kunali mamishonale ogwira ntchito ndi achinyamata. Ngakhale amawaphunzitsa sabata lilonse, iwo sanakhutire ndi momwe akhristu amakulira pang'onopang'ono. Iwo amaganiza kuti achinyamata ayambe kutumikira, ndiye anakhazikitsa lamuro loti okhaw omwe akutumikira ali oloedwa kutenga nao mbali pamaphunziro a pasabata. Achinyamata ambiri anayamba kutumikira muntchito zosiyanasiyana. Iwo amapanga ntchito zofikira mawanja ovutika mdera lao, kuphunzitsa ana ovutika (aumphawi), kuthandiza utumiki wa ana ndi zina. Pakutha pa miyezi yochepa mamishonale anadziwa kutiachinyamata ayambe kuzama pachikhulupiliro. Ndipo amafunika kuwerenga Baibulo ndikupemphera. Amafunika kukhulupilira Mulungu kuti akwanitse kuthandiza ena.

ZOKAMBILANA GULU LALIKULU

- Kodi zimachitika munkhani iyi ndizotani?
- Kodi achinyamata anayamba kutumikira munjira zotani?
- Kodi munaona anthu akukula pomwe ayambe kugwira ntchito yotumikira kudzera mu mpingo?
- Mukuganiza kuti anthu amakula akayamba kutumikira?

Kusintha Mabanja

Mpingo utha kuthandiza mabanja kukhala molingana ndi momwe Mulungu amafunira pophunzitsa mamembala mmene angakhalire ndi mabanja a mphamvu ndi momwe angakhalire makolo abwino, popeleka mpata kwa mabanja kuti apembedze ndikutumikira pamodzi. Mpingo ukuyenera kufufudza mpata othandizira anthu kuti athandize mabanja awo kukhala monga momwe Mulungu akufunira.

Kusintha Madera

Ngati mpingo titha kudzetsa kusintha munjira zambiri. Njira zitatu za momwe dera lingakhudzidwile ndi izi:

- **Kuchulukitsa Chiwerengero cha Akhristu**
Izi sikuti nthawi zonse ndikupanga tchalitchi kuti ikhale yaikulu. (Titha kupanga zimenezi pakuba nkhusa). Kuchulukitsa chiwerengero cha akhristu kumatanthauza kuti anthu omwe anali osakhulupilira akudziwa Mulungu ndikuvomereza Mkhristu ngati mpulumutsi wao. Mipingo imakhala ndi udindo othandiza anthu kuti amvetse uthenga ndi kulera (kusamalira) akhristu atsopano.
- **Kuphunzitsa anthu a mdera kukhala moyoomvera Mulungu**
Monga taphunzilira, Mulungu anatilenga ndipo akudziwazoyenera pa moyo wathu. Iye wationetsera mmene tikuyenera kukhalira mbaibulo. Titha kuphunzitsa ena zoyenera kuchita molingana ndi Baibulo. Ngati mpingo mutha kuyamba kusaka mpata othandiza anthu ena kumvera Mulungu mbali zonse za moyo wanu.

Ngakhale omwe alibe chidwi ndi chikhristu atha kukhala ndi chidwi chophunzira zaumoyo wao, kuti angakhale bwanji ndi banja lolimba kapena momwe angagwiritsire ndalama mwanzeru. Maphunziro a mtundu onga uwu amathandiza anthu kutukuka pa miyoyo yao, pomwe akukhala molingana ndi mfundo za mbaibulo ndikuthandiza kumanga maubwenzi pakati pa pomwe sali akhristu ndi mpingo.
- **Kuthandiza madera awo kukhala monga Mulungu amafunira kudzera pakuchita mapulojekiti**

MAGULU AANG'ONO

Yankhani Mafunso otsatirawa:

- Mateyu 20:28 –Kodi mchifukwa chiyani Yesu anadza?
- Afilipi 2:4-9 –Kodi Paulo akufotokoza motani za Yesu?

Yesu anabwera kudzatumikira. Makamaka, Baibulo likamati “pokhala muchilengedwecha Mulungu” atha kuwerengedwanso kuti, “chifukwa anali Mulungu, sanachiyesa cholanda kukhala wofana ndi Mulungu, koma anadzikhuthula yekha, natenga maonekedwe a kapolo.” Tangoganizani, chifukwa anali

Mulunguanadzikhuthula yekha kutenga maonekedwe a kapolo. Khalidwe la Mulungu ndi kutumikira. Monga mpingo uli thupi la Mkhristu, khalidwe la mpingo likuyeneranso kukhala kutumikira.

- Yakobo 1:27 –Kodi ndi chipembedzo chanji chomwe chimakondweretsa Mulungu?
- Marko 12:31 –Kodi Mulungu amatilamula kuti titani?

Chikondi chathu pa Mulungu ndi cha pa anthu oyandikana nao chikuyenera kutipangitsa kuti tikhale otumikira. Chimodzimodzi Mkhristu anabwera kudzatumikira, cholinga cha mpingo ndi kutumikira pothandiza anthu kuti adziwe ndi kukula mwa Mkhristu pakuonetsera chikondi chake kwa ena.

Pomwe tikutumikira mmadera athu tidzaona kuti akusinthika. Werengani nkhani ili munsimu ya mmene dera linasinthira pomwe mpingo unayamba kutumikira.

Sukulu ya Dera

Kagishu, tauni ina yodzala ndi nyumba zosalongosoka zopangidwa ndi malata otayidwa ndi matabwa ophwasuka, inali ndi mamembala khumi ndi asanu a mpingo. Mpingowu unaitanidwa nao kumaphunziro ena a utumiki ndipo unatumiza membala wao Meshack wazaka 21 kukakhala nao. Meshack anabwelera ndi masomphenya: “ndaphunzira kuti kumvera Yesu sikodzipereka!” Ndipo Meshack, Dismus (mkulu wampingo), Abusa ndi Mayi Abusa anapemphera, kumufunsa Mulungu kuti awapatse pulojekiti yomwe angaonetsera nayo chikondi ku dera lao. Yankho inabwera: yambani sukulu ya pulaimale ya ana a mu mpingo.

Posakhalitsa anayamba kulankhula ndi mamembala a mpingo omwe anali ndi ana koma saakwanitsa kupeleka ndalama yochepa ku sukulu ya Boma. Ambiri anavomereza kutumiza ana awo ku sukulu yatsopano iyi. Popanda maphunziro, Meshack, Abusa ndi akazi awo anayamba kuphunzitsa ana khumi ndi atatu, a zaka zapakati pa 6 ndi 12, mu chipinda chimodzi cha pa tchalitchiyo chopanda madesiki, mabuku ndi zipangizo zina. Anthu a mmudzi sanafune kuyanjanana ndi sukuluyo ndipo amkabwera usiku kudzaba zipangizo zomangira. Malipiro Oyamba a Meshack anabwera mwezi wa chisanu ndi chiwiri (7) – dola imodzi yopelekedwa ku fizi ndi zo0peleka zochokera kwa Makolo.

Meschack ndi Dismus anaitana ana a mmidzi yoyandikana nayo ndipo sukuluyo inakula. Posakhalitsa panali ana makumi anayi ndi asanu (45) a zaka zosiyanasiyana mkalasi imodzi. Mphunzitsi wachiwiri anadzipeleka mwezi wa chisanu ndi chimodzi ndi wachitatu mwezi wachisanu ndi chitatu. Ndi ana 100, aphunzitsi amkakhala pakati pa chipinda chophunzitsira, moyang'anizana makalasi awo. Posakhalitsa oyandikana nao anachoka. Atachoka sukulu inapeza mpata ochuluka. Pomwe sukulu imakwaniotsa zaka ziwiri inali ndi midadada iwiri, ndi zipinda khumi zomwe zikanatha kugwilitsidwa ntchito ndi mpingo lamulungu.

Chaka chotsatira mpingo unagula malo ku Kangware, inagula nyumba yokhazikika ndipo unasamuka. Mchaka chachisanu ndi chimodzi pasukuluyi panali aphunzitsi asanu ndi awiri olipilidwa, ndiena ogwira ntchito pasukuluyi asanu ndi ana 445.

Ichi ndi chiyambi chabe cha nkhani ya dera, sukulu ndi mpingo. Zotsatira zantchitoyi ndi zoti kuli sukuklu ya sekondale mmudzi wapafupi komwe kuli ogwira ntchito khumi ndi ana makumu asan ndi limodzi (60).

Mpingo wina unayamba sukulu ya mkombambala kwa ana makumi awiri omwe amayi awo amakhala akugwira ntchito. Mpingo oytamba omwe umkasonkhana unakula mkukhala gulu lalikulu la mamembala makumi asanu ndi limodzi (60) ndipo unadzala mpingo wina wa mamembala opitilira makumi anayi (40). Mpingo ulionse unatulutsa mipingo ina iwiri yatsopano mmalo osiyana.

Zaka zisanu ndi chimodzi zakudzipereka kwa mpingo waung'ono ndi mamembala ake pali zotsatira zozozeka Madera ndi mipingo ya dera ili. Makamaka kusintha ku Kagishu kunatsimikizidwa pomwe mamembala anaganiza zosintha dzina la deralo kuchoka ku Kagishu (lomwe limatanthauza “mpeni”) kukhala Ruita (kutanthauza kuti “kuchotsa chinachake choopsa”).

ZOKAMBILANA GULU LONSE/LALIKULU

- Kodi chinachitika munkhani iyi mchiyani?
- Kodi mpingo unali waukulu bwanji?
- Kodi zotsatira za ntchito yao zinali zotani?

Mmudzi wina munali chikhalidwe choti mbeu zikamakololelwa anthu amasonkhana ndi kuthandizana za kumunda. Ngakhale zinali chomwechi, munthu yemwe munda wake umakololelwa amayenera kukonza chakudya ndi chakumwa tsiku lilonse lomwe anthu angapite kukagwira ntchito kumunda wake. Mwatsoka, mtengo wa chakudya umatanthauza kuti mwini wake munda amapanga phindu laling'ono kwambiri pa zokolera zake.

Mpingo unaganiza kuti ngati ntchito zachifundo uthandiza mabanja osaukitsitsa mderalo kukolera minda yao popanda kalikonse ngati malipiro. Mmalo mwake amkabweletsa chakudya chao kudzadya nthawi ya nkhomaliro. Pomwe anthu ena a mdelari anayamba kuona mmene mpingo ukuthandizira osauka, anaganiza zoti athandizane popanda kufuna kufuna chakudya ndi zakumwa zambiri.

Pakadali pano anthu amathandizana kukolera mbeu zao. Palibe yemwe amayenera kupereka mowa ulionse kapena chakudya. Phindu lomwe alimi amapanga kuchyokera ku minda yao yakwera, ndipo zotsatira zake amakhala ndi chakudya chokwanira chaka chonse.

- Kodi mpingo unapanga zotani kuti uthandize derali?
- Kodi zinadzetsa kusintha kotani? Kodi zinadzetsa kusintha kotani mdera lonse?

ZOKAMBILANA GULU LALING'ONO

- Kodi ndi zinthu zina ziti zomwe mpingo wathu ungachite potumikira dera?
- Kodi mpingo wathu ungathandize bwanji anthu kukhala monga mwa chifuniro cha Mulungu?

Phunziro 7: Pulogalamu ya Truth Centered Transformation

Zolinga

1. Pulogalamu ya Truth Centered Transformation Program cholinga chake ndi kupeleka upangiri othandiza mipingo kusintha Madera awo.

Zipangizo

1. Masomphenya a pulojekiti
2. Posita ya Mpingo Osintha Dera
3. Mitu Yamaphunziro a Mtsogolo

Chiyambi

Uzani anthu awiri odzipereka kuti aime mbali zosiyana za tebulo. Auzeni kuti akokere tebulo mbali zosiyana. Pakutha pa mphindi imodzi kapena ziwiri, afunseni kuti aikokere mbali imodzi.

- Kodi mbali yosavuta ndi iti—kupita mbali imodzi kapena zosiyana?

Maphunziro awiri apitawo takamba za Ufumu wa Mulungu. Khumbo lathu ngati bungwe ndikuthandiza kumanga Ufumu wa Mulungu padziko lino lapansi. Masomphenya athu ndi (Kugwiritsitsa posita kapena kulemba pa bolodi):

Kuthandiza Mipingo Kusintha Madera Awo

Masomphenya athu ndi kuona zotsatira zopanga nanu mgwilizano. Pomwe mukumvetsera, lingalirani kuti kodi izi ndi zomwe inunso mukufuna kuti mugwire nao. Kumbukilani chitsanzo cha tebulo. Kodi inali yosavuta mbali iti? Pomwe anthu amapita mbali imodzi. mchimodzimodzi ndi kugwirira ntchito limodzi. Ngati tikufikira lingaliro losiyana ndiye kuti tikhumudwitsana. Sitingakhale abwenzi abwino. Tikagwirizana chinthu chimodzi kumanga ufumu wa Mulungu ndiye kuti tonse tikukankhira mbali imodzi. Tidzakhala pa ubwenzi wabwino.

Masomphenya a Pulojekiti

Kuthandiza Mipingo Kusintha Madera Awo

Kuthandiza Mipingo

Mu maphunziro athu a mbuyomu, mpingo umatenga mbali yofunikira kwambiri pomanga Ufumu wa Mulungu. Mpingo umapereka masomphenya ndi kuphunzitsa ndi kuthandiza anthu kuti agwire ntchito. Timakhumbira kuthandiza mipingo kukwaniritsa udindo wao. Sitikufuna kutenga/kulanda udindo wa mpingo. (Onetsani posita 5)

Kuthandiza mpingo sikutanthauza kuti:

- Tili ndi mayankho onse –dera ndi vuto lilonse limakhala lachilendo. Tiphunzira limodzi kuti tingathandize bwanji dera lanu moyenelera.
- Mukuchepekedwa kapena mulibe kuthekera— tili ndi matalenti, maluso ndi kuthekera kosiyana
- Kugwiritsa zones zomwe Mulungu wakupatsani, mutha kusintha dera lanu. Tikubweletserani maganizo ndi luso yomwe mungafune.
- Tikutsogolera zomwe zingachitike –uwu ndi mpingo wanu ndi dera lanu. Mukudziwa bwino zomwe zikuyenera kuchitika. Munjira yomweyo monga tinaperekera ganizo la ntchito za chikondi , tizipelekanso maganizo.Ngakhale zili chomwechi, monga zimakhallira ntchito za chikondi, sitikuuzani chilichonse choyenera kuchita. Mukuyenera kuganiza kuti ndi mapulojekiti otani ogwilizana ndi dera lanu.
- (IZI SIZINGAKHALE ZOYENERA PALIPONSE NDIPO ZITHA KUDUMPHIDWA) Tikuyamba chipembedzo kapena tikufuna inu kuti musinthe chipembedzo. Zotsemphana ndi izi ndi zoon. Timakhulupilira kuti musasinthe chipembedzo kapena kutsemphana ndi mtsogoleri wanu. Onani mmene Davite anachitira ndi Sauli: Davite anakhala ndi kuyimbira zeze Sauli ngakhale Sauli amamuponyera mikondo. Pomwe anali pachiposezo chotaya moyo wake, anachoka yekha. Sanayesele kutenga udindo wa Sauli kapena kufunsa anthu ena kuti achoke, ngakhale kuti Mulungu anamulonjeza kuti adzakhala mfumu. Pomwe anapatsidwa mpata, sanamuphe Sauli koma anamulora kuti akhale ndi moyo.

Timalimbikitsa anthu kuti atsatre chitsanzo cha Davite.Ngakhale mukuganiza kuti mtsogoleri wanu ndi ovuta mukuyenera kupitilira kumutumikira ndi kumupemphelera. Ngati zingafike povuta kwambiri mutha kuchoka nokha. Musatenge aliyense kupatula mkazi wanu ndi ana anu achichepere. Musalimbane ndi mtsogoleri wanu wakale. Monga Davite, tikuyenera kuopa ngakhale kulimbana ndi mtsogoleri.

Ngati atsogoleri a bungwe ili takhumudwa ndi momwe mipingo ina komanso atsogoleri ena amasinthira chipembedzo mwachangu. Sitimakhulupilira kuti zimalemekeza Mulungu. Sitikufuna kuti musinthe chipembedzo. Chonde khalani ngati Davite ndikukhala okhulupilika kwa atsogoleri anu ngakhale zikuoneka kuti ndizovuta. Izi zimalemekeza Mulungu

Monga bungwe sitimkakonderachipembedzo chilichonse komanso sitili a chipembedzo chilichonse. Timagwira ntchito ndi zipembedzo zosiyanasiyana. Mamembala a gulu lathu la atsogoleri amachokera ku zipembedzo zosiyanasiyana. Tikufuna mipingo yonse kukhala monga Mulungu amafunira. Tikukhulupilira kuti Mulungu atha kumanga Ufumu wake kudzera mu zipembedzo zosiyanasiyana.

Tanthauzo lake:

- Tikuphunzitsani momwe mungasinthire dera lanu. Sititumiza ogwira ntchito athu mdera lanu. Timakhulupilira kuti mpingo ndi chida chobweletsa chiyanjano ndiye tikufuna kukuthandizani kutsatira zolinga zake munjira iyi.
- Ndi masomphenya anu ndi mapulani anu. Tiyanbitsa maganizo ochuluka, koma zili ndi inu kusankha maganizo ndi mapulani omwe mungatsate pa mpingo wanu. Simukukakamizidwa kuchita ganizo lililonse, ngakhale muli ndi chidwi chofuna kuona Ufumu wa Mulungu mdera lanu, tikulimbikitsani kuti mukwanilitse mmene mungathere. Monga tayendera mipingo mu pulogalamu iyi taona kuti omwe agwiritsa ntchito zinthu zambiri (nzeru) aona kusintha kodabwitsa mdera lao. Omwe anapanga zinthu zochepa aonanso kusintha kochepa. Zili ndi inu malingana ndi kukhumba kwanu. Kuona dera lanu likusinthika kumafunikira kugwira ntchito molimbika.

Kusintha Dera

Gawo loyamba la masomphenya athu ndi kutukula mpingo. Gawo lotsatira ndi la zomwe tikuutukula mpingo kuti upange: kusintha Madera awo.

Kusintha

- Kodi mukuganiza kuti mchifukwa chiyani tikugwiritsa ntchito mau oti kusintha? Kodi mau oti kusintha amatanthauza chiyani?

Chinthu chikasintha, chonse chimasinthika kotero kuti sichingabwelerenso mbuyo. Mwachitsanzo, talingalirani za mbozi ndi gulugufe. Mbozi zimasintha mkukhala gulugufe. Zikatero sizitheka kubweleranso. Kumakhala kusintha kwathunthu ndipo kosabweleranso. Tikufunanso tione kusintha mmadera. Tikufuna tione Madera omwe asintha kwathunthu mkukhala monga mwachyifuniro cha Mulungu ndipo sakubweleranso mbuyo monga analili patatha zaka zochepa.

Magawo Osintha

MAGULU ANGO'ONOANG'ONO

Funsani gulu lililonse kuti liganize za kusintha komwe lingafune kuti kuchitike mdera lao panso pa mitu iyi –zauzimu, kuyanjana ndi anthu ena, maganizo ndi kuthupi –ngati zotsatira za pulogalamu iyi. Mukumbutse gulu kuti gawo la kuyanjana ndi ena likugwilizana ndi maubale mmonga; banja, makolo,

ubwenzi ndi oyandikana nao nyumba, umodzi ndi zina. Gawo lakuthupi muli zinthu monga; ndalama ntchito, thanzi ndi zina. Atha kuunikiranso maganizo omwe anaperekedwa mu phunziro 1.

Akamaliza aonetsere kukalasi zomwe akambilana. Kodi pali chilichonse chomwe chofanana chomwe guli lilonse lalemba kapena magulu ambiri alemba? Ndi chiyani?

Lembani tchatu yotsatira pabolodi. Funsani gulu kuti liyambe ndikuona mitu yomwe ili pansu pa kuyanjana ndi anthu ena, kaganizidwe, zakuthupi ndi zauzimu. Dutsani gawo lililonse kukambilana mafunso awiri pa mutu ulionse.

ZOKAMBILANA GULU LONSE

- Kodi pali kusiyana kotani pakati pa zolinga zomwe mwakonza ndi zomwe tatchula?
- Kodi pali zolinga zomwe tinatchula zomwe zinakudabwitsani kapena kuti simukugwilizana nazo?
- Mukamaliza kuyang'ana magawo anayiwa kambalanani:
- Pomwe mukuyang'ana pa ndandanda wa zolinga mukuona ngati pali kufanana kokwanira kuti tingathe kugwira ntchito limodzi?

Njira

Iyi ndi pulogalamu yamaphunziro. Sitipereka ndalama kumipingo kuti iyendetsele mapulogalamu. Monga tiphunzilire mu maphunziro otsatira, chifukwa chachikulu chomwe tili osauka sikusowa kwa zipangizo. Ndipo njira zomwe zingatitulutse mu umphawi sikulandira zipangizo. Mutayang'ana moyo wa Yesu, analibe chilichonse chopeleka kumbali ya zipangizo. Monga Petro ananera ku Machitidwe a Atumwi 3:6, “Siliva ndi golide ndiliba, koma zomwe ndili nazo ndikupatsa iwe.” Kumbali yathu tikupatsani nzeru ndi maganizo omwe tikukhulupilira kuti athandiza dera klanu kusuntha chifupi ndi momwe Mulungu amafunira. Tikukhulupilira kuti maphunzirop awa, kudzipereka ndi ndi kudzikhuthula kwanu, ndi mphamvu yodabwitsa ndi yochuluka ya Mulungu idzetsa kusintha mdziko lanu.

Timapereka maphunziro kwa aliyense mu mpingo kukuthandizani kuti mukhale ndi maganizo komanso luso lomwe likuthandizeni kubweretsa kusintha mmadera anu.

Mitu Yamaphunziro a Mtsogolomu

Gwirani posita 7 yoonetsa za mitu yamaphunziro otsatira. Fotokozani kuti iyi ndi mitu yomwe tikukonzekera kuphunzitsa, ngakhale kuti patha kupezeka kusintha.

Module 3 – Kodi Mabodza a Satana Amatikhudza Bwanji Ndipo Tingathane Nao Motani

Module 4 – Zaumoyo

Module 5 – Ukwati ndi Banja

Module 6 – Kasamalidwe Kandalama

Module 7 – Mchere ndi Kuwala

Module 8 – Zaulimi

Module 9 – Utumiki

Module 10- Kukhala monga Mulungu Amafunira

Ina mwa mitu –mwachitsanzo, Zaumoyo, Ukwati ndi Banja, Zaulimi ndi Kasamalidwe Kandalama – zikukhudza maphunziro a gulu laling’ono omwe atha kuchitika ndi mpingo onse komanso dera. Pomwe mukupanga maphunziro, tikuphunzitsani momwe mungagwiritsile ntchito maganizo awa kumpingo wanu ndi mdera lanu. Tikupatsani maganizo osiyanasiyana kuti mupange.

Phunziro 8: Zotsatira

Zolinga

- Tikuyenera kukonza mapulani ndikukhala ndi cholinga pantchito yathu.

Zipangizo

- Handout 8.1 Act of Love Planning Steps

Kodi Kukonzekera Mkofunika Motani

Bambo Lim, mlimi, anapita kukakonzeka munda kukonzekera kudzala koma ali munjira, anakumbukira zomwe anawauza akazi awo kuti adyetse nkuku, ndiye anapita kunyumba, kutenga zakudya za nkuku ndi kudyetse nkukuzo. Pomwe amadyetsa nkuku, anayang'ana mkhola mwa mbuzi ndipo anazindikila kuti khola linathyoka. Anakhumudwa kuti ngati siikonzedwa mwachangu ndiye mbuzi zikhoza kuthawa. Anabwelera kunyumba kukafuna waya okonzera khola. Chifukwa choti analibe zipangizo zoyenera, anapita kwa oyandikana nao nyumba, Bambo Son kukabwereka zipangizo. Chifukwa choti anafika kale kumeneko anaganiza zolankhula ndi Bambo Son omwe anali mkristu watsopano pa mpingo kwa mphindi zochepa, kamba koti anamva kuti sizikuwayendela.

Nthawi itakwana 11:30 mkazi wa Bambo Son akhalile limodzi pa nkhomalilo. Pozindikila za nthawi anapepesa ndi kubwelera kunyumba mwachangu kukadya nkhomalilo ndi banja lake. Atapumira pang'ono anapita kukamalizitsa kukonza khola la mbuzi. Pomwe amamaliza ntchitoyi, mkazi wake anamukumbutsa kuti pampu yamadzi pachitsime inasiya kugwira ntchito ndipo anaganiza kutinchifukwa choti anali ndi zipangizo za Bambo Son aikonzenso. Momwe tsiku limafika kumapeto, anatsala pang'ono kumalizitsa kukonza pampuyo. Apanso, anali asanapite kumunda kuja kukdzala, koma anamva kukhutitsidwa podziwa kuti tsiku lotsatira mammawa amafunika kuti amalizitse kukonza pampu ndikubweza zipangizo kenaka kuyamba dongosolo lodzala.

- Kodi chinachitika munkhani iyi ndi chiyani?
- Kodi zinthu zomwe anapanga ndi zolakwika kapena zoyenera?
- Kodi zotsatira zake zingakhale zotani ngati mlimi angapitilize kuyendetsa munda wake motere mpaka osadzala?
- Kodi munakhalapo ndi masiku ngati awa?
- Kodi tingaonetsetse motani kuti izi zisachitike kwa ife?

Mapulojekiti ambiri amayenda ngati tsiku ili la mlimi. Timapanga zinthu zambiri zabwino, kuchoka pa vuto kupita pa lina mpaka nthawi zina zinthu zofunika kwambiri sizimalizidwa chifukwa timaononga nthawi ndi kuchita zinthu zofunika. Zotsatira zake timalephera kukwanilitsa zinthu zofunika pamoyo. Zokhumudzitsa kwambiri ndizoti mitoyo yathu imayenda ngati ya mlimi. Timakhala otanganidwa ndi kuyenda kuchoka pamalo kupita pa ena posawelengera kuti chinthu chofunikira kwambiri ndichiyani ndikuchichita. Chinthu choyamba chomwe tikuyenera kulingalira ndichomwe chili chofunika kwambiri

kuchita. Ngati tikudziwa chomwe chili chofunika ndiye kuti zitithandiza kupanga maganizo oyenelera a mmene tingagwilitsire ntchito nthawi yathu.

Kodi mukuganiza kuti zinthu zofunika kwambiri kupanga miyezi itatu yotsatira ndi chiyani kuti mupambane?

Kuphunzitsa ena –ngati tikufuna kuti ziwalo za thupi zitumikile tikuyenera kuphunzitsa ena mwa maphunziro omwe taphunzira kale.

- Kulumikizitsa ntchito za chikondi –tikuyenera kupitiliza kupanga ntchito za chikondi pafupipafupi.
- Kukumana pafupipafupi

Mikumano

Mukuyenera kusankha gulu ndikukhala pamodzi pafupipafupi kukonza mapulani a ntchito za chikondi. Mwachizolowezi iyi ndi komiti ya pampingo ndipo imatha kuchitika nthawi ya mikumano ya komiti ya mu mpingo, ngati komiti ya pampingo imakumana kale nthawi zingapo pamwezi.

- Kodi zinthu zomwe mukuyenera kuchita mukakumana ndi zotani?
 - KUWALA –ndi mu mphamvu ya Mulungu yokha yomwe ingatipangitse kuona kusintha kwa madera athu.
 - Tikuyenera kukhala pamodzi mmapemphero ngati tafunitsitsa kusintha.
 - Pangani maganizo a ntchito za chikondi a tsopano.
 - Ganizani za zomwe mungachite kuti muthandize dera lanu.

Pa mikumano yanu khalani ndi nthawi yopemphera ndikukambilana zofunikira mdera lanu. Pempherani ngati mungathandize komanso kuti mungathandize motani. Moonjezera mukhale ndi nthawi younikira ntchito ya chikondi yomaliza ndikuona zomwe zinayenda bwino komanso zomwe sizinayendee bwino. Dzifunsemi nokha kuti nthawi ina mungapange motani.

Ntchito za Chikondi

Tayang'anani chithunzi cha dera lanu chomwe munapanga mu phunziro 1.

Kuyang'ana zithunzi zones, pangani ndandanda wa zinthu zikuluzikulu zomwe tikufuna kuti zichitike kupanga chithunzi chilichonse kukhala choona.

Monga gulu pempherani momwe mungayambire kupanga chimodzi mwa zosinthazo kukhala zoona. Sankhani chimodzi mwa zosintha ndipo limodzi ndi pulani ya ntchito zachikondi kuthandiza kubweletsa izi.

OnaninsoFomu ya Pulani ya Ntchito za Chikondi (tsamba lotsatira) ndipo konzaninsio pulani.

MACHITACHITA A CHIKONDI- MNDANDANDA WA ZOCHITIKA

Sitepe Yoyamba : Pemphero

Chinthu choyamba kuchita ndiko kupemphera . tengani nthawi yanu kupemphera . Funsani Mulungu kuti akuonetseni kuti ndi chiyani chomwe mungachite pa ntchito yanu ya chikondi.

Sitepe Yachiwiri: Kusankha chochitika.

Monga Gulu , taganizilani chimene mungachite kuti muonetse chikondi cha Mulungu. Tayang'anani ziganizo zina zomwe zomwe munatchula mu phunziro loyamba ndikugwilizana chomwe mukuganiza kuti Mulungu akukutsolerani kuti muchite.

Mukati mwasankha mutu , muonetsetse kuti chikhale chinthu chomwe mungachipange mu tsiku limodzi kapena awiri. Ngati sizingatheke , mungochita sitepe yoyamba ndi yachiwiri yokha basi?.

Sitepe yachitatu: taganizani chimene chikufunika.

Sitepe yotsatira ndiko kuyamba kuchita ndondomeko. Koyamba tikuyera kuganizila zimene tikufuna kuti pa Polojekiti- ndi anthu ati amene akufunikila , ndi zida ziti , ndi ndani akuyenera kupeleka chilolezo. Ndi zina zotero. Kuthandiza kuti muganizile ichi , mutha kugwilitsa ntchito dongosolo la kagwilidwe ka ntchito limene lili mu buku la ophunzira. Mukamaliza ku fila ndime yoyamba ndi chinachilichonse chomwe mukufuna , ndiye mutha kuganizila kuti ndi ndani amene achite ntchito ndiponso tsiku lanji lomwe mukhale zonsezi mutamaliza.

Sitepe yachinayi: lembani ndondomeko.

Mukatha kukonza ndondomeko ya chilichonse chomwe chikuyenera kuchitika ,tsopano mutha kulemba pulani yanu molingana ndi ma tsiku . cholinga choti mudziwe kuti ndi ndani amene adzachitwe chiyani pofikila liti.Tsankhani munthu munthu mmodzi kuti akhale otsogolera pulojekiti imeneyi. Munthu ameneyu akhala oyenera kuwapeza anthu kapena kulumikizana nawo pa tsiku limene akuyenera kukhala atamaliza kufuna kuona ngati ntchito ikugwilika , ngati pali mabvuto ena , kapena ngati akufuna thandizo lina lililonse.

Sitepe 5: Pemphero

Mukamaliza kulemba ndondomeko yan , teganinso nthawi yopemphera. Mufunsani Mulungu kuti akuthandizeni kumalizitsa ntchito ndikuchulukitsa zotsatila , kuti dzina lake likalemekezeka. Mu tsabata yotsatila kapena awiri pamene mukukonzekera ntchito zan za chikondi , mukuyenera kumapemphera kuti Mulungu akuthandizeni ndi zochitikazo.

Sitepe 6: CHITANI NTCHITO YA CHIKONDI

Chotsatila ndiko kuchita ntchito ya chikondi imene mwakonza . yambani tsiku lanu ndi pemphero ndikupeleka mphanvu zanu kwa ambuye. Kumbukilani kuti mukuchita izi kuti muonetse chikondi cha Mulungu ku dera lanu. Yetsetsani kukhala ndi chidwi kuti zotsatira zimenezi mudzifikile basi.

Sitepe 7: Kauniuni wa mmene ntchito yayendera ndikupeleka ma lipoti:

Sitepe yomaliza ndiko kuunikila ndi kupeleka lipoti . kodi ndi chifukwa chiyani chomwe tikuyenera kuchitira zimenezi?. Chifukwa imatithandiza kuphunzira , titha kuganiza zimene tinachita bwino ndi zimene titha kukonza nthawi ina. Sikuyenera kukhala ntchito yaikulu, mutha kutenga mphindi zochepa kukambilana mafunso amenewa:

- Ndi chiyani chimene chinayenda bwino?.
- Ndi chiyani sichinayende bwino?.
- Kodi ndi pati pamene mungakonzere nthawi ina?.
- Kodi anthu anazilandila mmene mumafunila? Ngati sichoncho ndi chifukwa chiyani?.
- Kodi Mulungu analemekezeka?

Amene akukuphunzitsani ali ndi fomu yolembela lipoti yanu , kodi ndi chifukwa chiyani timalemba lipoti?. Mu Marko 6:30 tikuona kuti ophunzira a yesu akupeleka lipoti kwa yesu pa zonse zimene anapanga. Timapeleka lipoti monga kukhulupilika ndikuthokoza kwa iwo amene anatiphunzitsa ndikukonza zida zofunikila komanso kutikonzero aphunzitsi. Lipoti imakupatsani mwayi kuti muonetse ena zimene munapanga ndi kuchitila umboni za mmene Mulungu anagwilitsa ntchito mphanvu zanu. Limapelekanso mwayi kwa ophunzitsa kuti aone ngati pali bvuto linalililonse ndikukwanitsa kukuthangatilani in bwino patsogolo.